
# KUFA, KUUKA NDI KUKWERA KUMWAMBA KWA YESU KHRISTU

**Malongosoledwe a Baibulo wogwiritsa ntchito panokha kapena pa gulu**

**Lolembedwa ndi Fred Morris**

**Lotanthauzilidwa ndi Lapson Mbewe**

**Revisão por: Steven Kaombe**




## MARKO GAWO 2

## Mutu 9 to 16

Manna Publications

**Kwa Owelenga kapena Atsogoleri**

Mabukhu awa amalongosola za Bible mu choonadi chokhudza mau a Mulungu mwandondomeko ndi ndi muchilankhulo chomveka bwino kuwelenga. Mabukuwa mungathe kuwagwilitsa ntchito panokha kapena ndi anzanu pagulu. Pamene mukugwilitsa ntchito mabuku awa ndikwabwino kwambiri kuti aliyense akhale nalo buku lake ngati kungatheke kutero. Ndikungothokoza Mulungu chifukwa cha moyo umene ndili nawo komanso a Manna Publications chifukwa chondipatsa mwai womasulira bukuli mu Chichewa chilakhulidwe chimene ndinabadwa nacho.

**Dziwani izi:** Pamene mungapeze chizindikiro ichi, chikusonyezani inu kapena mtsogoleri wa gulu kuti akuyenera kuwelenga Bible mokweza musanayambe kukambirana mau onse a buku ili.

**Kambiranani za izi:** Paliponse pamene mwapeza chizindikiro ichi ndiye kuti pali mafunso othandiza kuona ngati owelenga akutsatira abwino zimene akuphunzira. Mafunso omwewa mungathe kugwilitsa ntchito ngati mayeso.

**Mabokosi ophunzisira odulidwa nzele:** Pamene mwaona izi, uthengawu ukupereka maphunziro oyenjezera okhuza moyo panthawi imene ndime ya m’baibulo inkalembedwa komanso ndikuthandiza kaphunzisidwe kalero.

**Kuyamikira:** Mawu a m'Baibulo, otengedwa mu HOLY BIBLE New International Reader's Version, ndi ovomerezeka © 1996, 1998 by International Bible Society. Inaperekedwa panthawiyo ndi chilolezo cha Hodder & Stoughton Ltd., membala wa Hodder Headline Group. Maumwini onse ndi otetezedwa. Onani pa intaneti pa: www.biblestudytools.com/nirv

Zithumzi ndi Zokopera © Global Recordings Network (GRN). Kugwiritsa Ntchito Chilolezo.

---

**Mark Part 2 © 2002, 2020, 2024, Fred Morris, Manna Publications (USA) Inc. Todos os direitos reservados.**

**Deus nos permitiu imprimir este título nos seguintes países:**

***Edição mundial revisada em inglês publicada pela primeira vez no Reino Unido em 2002***

Reimpresso 2003: Quénia (swahili), Moçambique (inglês da Suazilândia), Índia (tamil), Etiópia (amárico). 2004: Quénia, Uganda (inglês), Quénia (dinka para o sudão), Malawi (chichewa), Etiópia (amárico). 2005: Uganda (inglês, lingala para a Rep Dem do Congo), Quénia (dinka para o Sudão), Mianmar (inglês, khumi chin), Quénia (bari para o Sudão). 2006: R.D. Congo (lingala), Serra Leoa, Tanzânia, Libéria (inglês). 2007: Quénia, Nigéria, Uganda (inglês). 2008: Burundi (kirundi), Índia (telugu), Mianmar (tiddim chin). 2009: Tanzânia, Libéria (inglês, suaili). 2010: Mianmar (inglês, dai, birmanês, tiddim chin), Moçambique (português), Reino Unido (inglês), Etiópia (oromo). 2011: Índia (telugu, tamil, inglês), Burkina Faso, Camarões (francês), R.D. Congo, Katanga (francês, kiluba, kisongye), Guatemala (espanhola), Myanmar (birmanie), Nigéria, Uganda (inglês) 2012: Serbia (serbio), Paquistão (saraiki), R.D. Congo, Katanga (kiluba, francês), Camarões (inglês), Nigéria (inglês), Índia (hindi, telugu, tamil, oriya, inglês). 2013: Camarões (inglês, francês), Índia (tamil, francês), R.D. Congo, Katanga (português), Etiópia (sidama, oromo), África do Sul (refugiados congoleses), Sierra Leone (inglês). 2014: Moçambique (português), Quênia (swahili), Camarões (inglês), Arménia (arménio). 2015: Gana (inglês), Mianma (ngawn chin, hakha chin, birmanie), Malawi (chichewa Braille, inglês Braille), Camarões (inglês, francês), Etiópia (oromo). 2016: Malawi (chichewa), Etiópia (amharic, oromo), Mianma (hakha chin, ngawn chin), Malawi (inglês Braille). 2017: Sierra Leone (inglês). 2018: Índia (kannada), Malawi (chichewa), Mianma (birmanie), Camarões para a África Equatorial (espanhol). 2020: Uganda (inglês), Malawi (chichewa), Arménia (arménio), Moçambique (português). 2022: Moçambique (portugués), Arménia (arménio), Índia (kannada), Malawi (chichewa). 2023: Malawi (chichewa). 2024: Malawi (chichewa)


# MARKO GAWO 2

## Mutu 9 to 16

## OKONDEDWA AWERENGI

Mu bukhu lathu loyamba la ndemanga pa uthenga wa Marko (Marko 1-8) tinanena za zozizwitsa zimene Yesu adachita. Akhristu amakhulupirira kuti Iye anali 'mwana wa Mulungu'. Ngakhale anali Mwana wa Mulungu, Yesu adaleredwa ndi Yosefe wokhoma matabwa wa ku Nazareti, mdziko la Israeli. Yesu anadzitchula yekha kuti anali 'mwana wa Munthu'.

Tikuyamba mbali yachiwiri ya moyo wa Yesu Khristu pamene akuyandikira mapeto a zaka zitatu za chiphunzitso ndi machiritso Ake. Izitu zinachitika pafu fupi zaka zikwi ziwiri zapitazo. Mugawo loyamba tinanena kuti Yesu anaphunzitsa kupyolera mu mafanizo ambiri za Ufumu wa Mulungu. Mafanizo ndi nthano zonena zimene anthu angathe kuzimvetsetsa mosavuta, popeza amagwiritsa ntchito zinthu zowoneka za m'moyo powonetsa chilungamo cha Mulungu.




**A linhagem familiar de Abraão a Jesus Cristo (Mateus Capítulo 1)**

Tinanenanso za omutsatira Yesu kuti anakhulupirira kuti Iye anali Mesiya, kapena Khristu. Ayuda mu Israeli anadikira kwa zaka zambirimbiri kubwera kwa Mesiya. Anali Mpulumutsi wolonjezedwa amene Mulungu analonjeza kuti adzapulumutsa anthu ake. Aneneri ananenanso za Iye kuti adzabwera. Analemba za Iye mu zolembera zopatulika-Chipangano Chakale cha Baibulo.

Anthu ena amene anamtsata Yesu anaganiza kuti iye anadza kudzapulumutsa anthu kwa adani awo, Aroma. Koma Yesu, Mesiya, anadza kudzakhazikitsa ufumu watsopano pa dziko- ufumu wa wokhulupirira amene adzadalira ndi kumvera Mulungu ndi Yesuyo. Sanadze kuti adzapulumutse anthu kwa olamulira a Chi Roma ayi. Anadza kudzamasula anthu ku machimo awo- njira zawo zoyipa- kuti akamudziwe Mulungu ndi kukhala mbali ya Ufumu Wake kuli konse

kumene iwo angakhale, ndi kuti akakhale ndi moyo wosatha Kumwamba pamodzi ndi Iye.

Tanthauzo la dzina la Chihebri loti Yesu (Yeshua) ndi ‘lakuti mpulumutsi wa Mulungu’. Aneneri ambiri analemba za lonjezano la Mulungu kwa anthu lakuti adzawapatsa Mpulumutsi wobadwira mdziko la Israeli. Anthu adawerenga zolembedwa zopatulikazi zonena kuti Iye adzachokera mumbadwo wa Abrahamu, Isake, Yakobo (Israeli) Yuda ndi mfumu Davide. Iye ananenedwa kuti adzapulumutsa a Yuda onse ndi dziko lonse ngati anthuwo adzakhulupirira Mulungu ndi Iye monga Mesiya.

Akhristu amakhulupirira kuti Yesu ndi Mpulumutsiyo Mesiya wonenedwayo koma Ayuda ndi Aluya ambiri sakhulupirira kuti Yesu ndi Mwana wa Mulungu. Iwo akudikirabe Mesiya kuti abwere.

Tinakuwuzaninso kumapeto kwa gawo loyambali kuti Yesu anawapatsa Akuphunzira Ake chenjezo. Iye anati adzanzunzidwa kwambiri ndi kuphedwa kuti iwo akapulumutsidwe. Izi ndi zina mwa zinthu zambiri zonenedwa mu zolembedwa zonena za Mesiya. (Makamaka pa Yesaya 53) Zinthu izi zidalembedwa zaka mazanamazana Mulungu asanatumize Mwana Wake. Tikhoza kuwerenga za zinthu izi mu Baibulo lathu ndi kuwonanso mmene zinakwaniritsidwira.

## 🕮 Werengani: Marko 9:1

## UFUMU WA MULUNGU

Mu ndemanga ya Baibulo ino Marko 9-16, tikuwuzani za kupachikidwa, kuwuka, ndi kukwera ku Mwamba kwa Yesu Khristu. Izi zikutanthawuza m’mene Yesu adafera, m’menenso adakhalira wa moyo ndi kubwerera ku Mwamba.

Ichi chinali chikonzero cha Mulungu pofuna kupulumutsa dziko ku chilango chobwera ndi uchimo. Apa ndiye kuti omutsatira Yesu atha kukhululukidwa machimo awo ndi kupita ku Mwamba kukakhala ndi Yesu kwa muyaya.

Gawo lachiwiri lino tiliyamba ndi vesi limodziri, limene ndi mbali ya mawu onenedwa ndi Yesu. Apa Yesu anali kuwuza omutsatira (Akuphunzira Ake ndi khamu la anthu) kuti anthu ena ambiri adzaziona zinthu zimene Mulungu adalonjeza kuti zidzachitika, zikuchitika. Izi zidalembedwa ndi aneneri ndipo zidzathandiza kuti anthu akonzekere kubwera kwa Ufumu wa Mulungu.

Kwa zaka mazana anayi, Mulungu anakhala osalankhula ndi anthu Ake kupyolera mwa aneneri. Mulungu adadikira nthawi yabwino yakuti atumize Yesu pa dziko lapansi. Kenaka Mulungu adawonetsa mphamvu Yake yodabwitsa kupyolera mwa kupachikidwa, kuwuka ndi kukwera ku Mwamba kwa Yesu kudzanso zina zodabwitsa zimene zidawoneka pambuyo pake. Mnjira imeneyi, Mzimu Woyera anali kumanga maziko a Ufumu watsopano mu miyoyo ya onse otsatira Yesu Khristu-Ufumu wa Mulungu.

Chotsatira chimene Marko akutiwuza, ndi m’mene Mulungu adamukonzetsera Yesu kukumana ndi zochitikazi.

**Kudza kwa Ufumu wa Mulungu**

Zinthu zina zimene Yesu adadziwa kuti zidzachitika ndi izi:

- Kupachikidwa ndi imfa ya Yesuyo ndi kuti mwazi Wake udzakhala nsembe yolandirika ndi Mulungu kuloza ku chikhululukiro cha machimo a wanthu olapa ndi kusiya machimo awo.
- Kuwuka kwa Yesu kwa akufa (Mdzukiro) kupita kumoyo wosatha idzakhala mphatso ya Mulungu kwa anthu onse okhulupirira Mwana Wake.
- Kukwera kwa Yesu kupita ku Mwamba kumene adzakhala ndi Mulungu Atate komwe Ali kukakonzetsera malo kwa onse okhulupirira (Yohane 14:2).
- Kutumizidwa kwa Mzimu Woyera wa Mulungu (pa Pentekoste) kudzathandizira okhulupirira kukonza njira ya Ufumu wa Mulungu ndi mphamvu pakati pa amitundu yonse. (Werengani bukhu la Machitidwe).
- Kupasulidwa kwa Kachisi wa Mulungu wa padziko la pansi (Kudachitika mu Yerusalemu mu chaka cha AD 70 ndi nkhondo) kusonyeza kuti Mulungu tsopano azikhala mu mitima ya okhulupirira osati mu akachisi kapena m'nyumba zopembedzera-tchalitchi (1 Akorinto 3:16).

## Werengani: Marko 9:2-13

## YESU AWALA NDI KUWALA KOPOSA

Itapita sabata imodzi Yesu anatenga Petro, Yakobo ndi Yohane nakwera paphiri lalitali (9:2). Mwinatu iri linali phiri la Heremoni limene linali lokwera mikono zikwi zitatu. Uka amati adakwera pamenepo kukapemphera popeza anali malo achete kumene sikumafikako anthu.

Akuphunzirawa anamuyang'ana Yesu. Tawonani nkhope Yake inawala ndi kuwala kwa Kumwamba. Akuphunzira adalephera kumupenya kwa nthawi yayitali. Kuwala kwa Ulemerelo Wake kunali konga mphenzi, kwa mphamvu ndi kosatheka kwa kanthawi (Luka 9:29). Zovala zake zinawalanso momwemo.

Akuphunzirawa anawona anthu enanso awiri-Mose ndi Eliya, nawonso ali wowala chimodzimodzi. Awiriwo anabwera kudzalankhula ndi Yesu za imfa Yake ya ku Yerusalemu (Luka 9:31).

## MULUNGU AYANKHULA PAMWAMBA PA PHIRI

Pamene akuphunzira atatuwo anali kukamba za izi, mtambo owala unawakuta. Mtambo oterewu udakutanso Mose kale, pamene Mulungu adalankhula naye pa phiri (Eksodo 19:18). Petro adawuma pakamwa kusowa chonena (Marko 9:6). Petro adafuna kulankhula m'malo momvetsera.

Mawu a Mulungu adamveka kuchoka mu mtambo ndi kuti: 'Uyu ndi Mwana Wanga Wokondedwa. Mverani Iye!' (9:7). Akuphunzira anachita mantha akulu

nagwa pansi kubisa nkhope zawo. Anaweramitsa nkhope zawo pansi chomwecho kufikira Yesu anabwera nawakhudza iwo.

'Mukani. Musawope', Yesu anawawuza (Mateyu 17:7). Atagalamuka anapeza kuti anali okha ndi Yesu. 'Musawuze wina ali yense', anatero Yesu, 'kufikira Mwana wa Munthu atauka kuchokera kwa akufa' (9:9). Kuyambira nthawi imeneyo Yesu ananena za kufa kwake ndi kuwuka kwake pafupi pafupi (9:9, 12, 31; 10:33, 34, 45; 12:8; 14:8).

Nkhani ija ya kuwala kwa Yesu kochokera kwa Mulunguku, imatchedwa 'Mawalitsidwe a Yesu'. Mawalitsidwewa adasonyeza kuti:

- Yesu ndi mwana wa Mulungu. Mulungu adanena choncho kwa Petro ndi Yakobo ndi Yohane.
- Yesu anali ku Mwamba asanabadwe ngati mwana. Yesu adamudziwa Mose ndi Eliya amene adakhalapo zaka zambiri zapitazo.
- Mose ndi Eliya adadziwa kuti chinali chikonzero cha Mulungu kuti Yesu adzafe. Analitu kukamba ndi Iye (Yesu) za imfa Yake.

Mulungu adachita izi kuti amulimbikitse Yesu asadafe. Petro adalemba za mawalitsidwewa zitapita zaka zingapo (2 Petro 1:17, 18).



**Jesus brilhando com uma luz brilhante do céu com Moisés e Elias**

**Kambiranani**

1. Ndi chifukwa chiyani Yesu adawalitsidwa pamaso pa akuphunzira?
2. Kodi mawu amene adamveka paphiri paja anali andani ndipo adati chiyani za Yesu?
3. Kodi Petro, Yakobo ndi Yohane adachita mantha chifukwa chiyani?
4. Kodi nkhani ya kuwalitsidwa kwa Yesu idatsimikizanji za Yesu?
5. Kodi nthawi zina timayankhula m'malo momvetsera?

# YOHANE MBATIZI ADALI WOYAMBA

Zolembedwa zopatulika zikutiwuza kuti munthu wina adzabwera 'mu mzimu ndi mu mphamvu ya Eliya' (Malaki 4:5-6). 'Eliya adabwera poyamba', Yesu adawawuza akuphunzira ake. Uyu anali Yohane Mbatizi.

Yohane adalalikira 'mumzimu ndi mumphamvu ya Eliya' ndipo adabweretsa anthu ambiri mu Israel kwa Mulungu, Ambuye Wawo. Adawakonzetsera anthuwo kubwera kwa Ambuye Yesu. Yohane anali ndi mzimu ndi mphamvu imene Eliya anali nayo.

Adawaphunzitsa anthu amene sanali kumvera Mulungu. Anawawuza kuti akhale anzeru ndi kuchita chimene chinali cholondola. Potero adatha kuwathandiza anthuwo kukonzekera kubwera kwa Yesu (Luka 1:16, 17). Koma Ayuda ambiri maka atsogoleri awo, sanakhulupirire kuti Yohane anali m'neneri wotumidwa ndi Mulungu ndipo Mfumu Herode adamupha.

Ayudawa sanakhulupirirenso kuti Yesu anali Mwana wa Mulungu. Kwa iwowa Yesu anati: 'Ufumu wa Mulungu udzachotsedwa kwa inu ndi kuperekedwa kwa anthu amene abala chipatso…' (Mateyu 21:43) 'Chipatso' chitanthawuza kukhulupirira ndi kuchita ntchito imene isangalatsa Mulungu.

Panthawi imeneyo ambiri a wanthuwo anakhulupirira kuti Eliya adzabweranso Mesiya asanabwere. Chotero sichinali chodabwitsa kuti akuphunzira anamufunsa Yesu za Eliya makamaka pamene adamuwona pa phiri paja ali ndi Mose. Onani kuti funso lisadafunsidwe, Yesu adakamba za kuwuka Kwake. Poyankhanso funsolo, Iye akunena za kunzunzidwa kwa 'mwana wa Munthu'-dzina limene anali kukonda kugwiritsa ntchito ponena za Iye mwini.

### Kambiranani

1. Ndi chifukwa chiyani aphunzitsi a chilamulo adanena kuti Eliya ayenera kuyamba kubwera (9:11)?
2. Yesu anali kutanthawuza chiyani pamene adati Eliya anabwera kale?
3. Yesu adadziwa bwanji kuti adzanzunzidwa, kufa ndi kudzakhalanso ndi moyo (9:9)?
4. Ndandalikani zinthu zonse zimene Petro, Yakobo ndi Yohane adaphunzira za Yesu.

## Werengani: Marko 9:14-31

## MWANA (MNYAMATA) WOGWIDWA NDI MZIMU WOSALANKHULA

Bambo wina adadza kufuna Yesu kuti athandize mwana wake amene sanali kutha kumva ndi kuyankhula. Mzimuwu udayamba ali mwana. 'Udali kumuponya iye pamoto mwina pa madzi kuti umuphe.' adatero bamboyo (9:22).

Yesu anadza kwa Akuphunzira pamene anali kuyankhula ndi khamu losonkhanapo. 'Kodi mukangana ndi Afarisi za chiyani?' Iye adawafunsa.

Bambo wa mnyamatayo adayankha ndi kuti 'Ndabwera ndi mwana wanga amene ali nawo mzimu woyipa ndinawafunsa Akuphunzira Anu kuti awutulutse koma alephera' (9:17-18).

'Wadwala kwa nthawi yayitali bwanji?' Yesu adafunsa. Bamboyo adafotokoza mavuto amene adakomana nawo:

- Iye anali kulephera kuthandiza mnyamatayo.
- Iye (bamboyo) adadikira kwa nthawi yayitali kuti abwere kwa Yesu.
- Iye anali wokonzeka kutaya chiyembekezo chake.

# CHIKHULUPIRIRO CHOCHIRITSA

Ife monga otsatira a Yesu, tiyenera kuyembekezera kuti zowoneka ndi zotichitikira zikhala ngati mapiri tikakhala ndi Mulungu. Tikumananso ndi nthawi zovuta pamene mizimu yoyipa idzalimbana nafe. Chikhulupiriro chathu podalira pa Yesu chimayesedwa.

Tikhoza kugonjetsa Satana ndi mizimu yake yonyansa pamene mphamvu ya Yesu ikhala nafe (Luka 10:19, 20).

Wokhulupirira amene apulumutsidwa ndi Yesu ayenera kuyankhula mu dzina la Yesuyo.

Tikhoza kuwateteza ana athu powapempherera iwo kuti mphamvu ya Ambuye Yesu, amene adakhetsa mwazi Wake pamtanda, iwapulumutse. Mulungu safuna kuti wina aliyense wa tiwana ngati timeneti tikatayike (Mateyu 18:14).

Tiyenera kuwapempherera ana athu kawirikawiri. Komanso tiyenera kuwachotsa iwo pakati pa anthu oyipa, pa malo pamene pamakhala zoyipa. Tisawalorenso kuwerenga mabukhu onena zonyansa ndi kuwonera akanema olawula, zimene zingapangitse Satana kuti awagwiritse ntchito.

Mphamvu ya Mulungu yochiritsa ndi kupirikitsa mizimu yoyipa imapatsidwa kwa iwo wokhulupirira amene apemphera mu dzina la Yesu, mu mwazi wa Yesu. Koma chikhulupiriro chimafunikiranso.

'Uyenera kukhulupirira' Yesu adamuwuza bambo wamwana uja. Iye adafuwula 'Ndikhulupirira!'. Anawonjezeranso mwamsanga pemphero 'Thandizani kusakhulupirira kwanga' (9:24).

Tonse tiyeneranso kupemphera monga adapempherera bamboyu. Mulungu ali wokhoza kutichitira ife chirichonse, koma tiyenera kukhulupirira!

Pamene Yesu adawona khamu la anthu akudza mothamanga kudzawona chimene chinali kuchitika (9:25) anati kwa mzimu wonyansawo:

'Mzimu wosalankhula ndi wogontha iwe, Ine ndikulamula iwe, tuluka mwa iye, ndipo usalowenso mwa iye'.

Yesu sanafune kuti khamu lidzawone izi. Podzudzula mzimuwo, Iye adawutchula dzina. Mzimu woyipawo udamuponya pansi mnyamatayo, ndipo kenaka udatuluka mwa iye. Anthu atawona m'myamatayo ali gone adayesa wafa.

'Wafa', iwo adanena wina ndi mzake (9:26). Koma Yesu adagwira dzanja lake namunyamutsa (9:27).

Izi zidachitika patangotsala masiku ochepa kuti Yesu aphedwe. Tiyenera kuphunzira mosamalitsa zimene Yesu adawaphunzitsa Akuphunzira Ake mu masiku otsiriza a moyo Wakewa. Apa Iye adati: 'Chiri chonse chiri chotheka kwa iye amene akhulupirira' (9:23).

Palibe vuto limene liri lomulaka Mulungu (Genesis 18:14). Chinthu chovuta kwambiri chisowekanso chikhulupiriro chochuluka, chinthu china chisoweka

kulimba mtima kopambana. Zinthu zina zifunika kudekha kwambiri, zina zisowa nthawi yayikulu kuti zitheke.

Chofunika ndi kugwiritsa, kupempha mwa chikhulupiriro ndiponso kuwona Mulungu akugwira ntchito yochitira ife ubwino mu zonsezi. (Aroma 8:28). Tisagwetsedwe mphwayi, tisataye chikhulupiriro.

**Kambiranani**

1. Ndi chifukwa chiyani akuphunzira analibe mphamvu yotha kumuchiritsa mnyamata wodwalayo (9:18, 19, 29)?
2. Bambo wa mnyamatayo ananenanji kwa Yesu (9:22)? Kodi inu nthawi zina mumamva chimodzimodzi?
3. Kodi yankho la Yesu linali lotani (9:23, 29)? Akunenanji kwa inu pamene muli ndi chosowa?
4. Pamene mukumana ndi Mulungu pamodzi ndi okhulupirira ena, mumakonzekera bwanji zovuta zimene zingathe kukutsatani?

## AKUPHUNZIRA SANAMVETSA ZA YESU

Yesu ananena za kupachikidwa ndi za kuwuka kwake. Anawatengera Akuphunzirawo kumbali kwa okha nawaphunzitsa za zinthu izi (9:30-31). Akuphunzira sanathe kumvetsa zomwe ziti zidzachitike. Iwo anawopa kumufunsa Yesu za zinthu izi (v.32). Pamene ife sititha kumvetsa, timakhala ndi mantha. Akuphunzira akadamudziwitsitsa Yesu, akadatha kumvetsetsa zambiri zokhudza Mulungu. Iwo akadatha kumvetsetsa chifukwa chimene Yesu adadzera pa dziko, kudzanzunzidwa kuti apulumutse anthu. Baibulo limati Yesu ndi, Mtumiki wosautsidwa (Yesaya 53:3-6; Afilipi 2:6-8). Akuphunzira anayenera kuphunzira zambiri zonena za Yesu kuti iwo athe kufanana ndi Iye.

## Werengani: Marko 9:33-41

## NDI NDANI WAMKULU?

Ndipo Yesu adatenga mwana wamng'ono ndi kumuyimika pakati pawo (9:36). Apa nkuti Yesu atangonena zoti adzaphedwa, koma Akuphunzira anali kukangana pakati pawo kuti wamkulu anali ndani! Iwo sadamvetsere ndi kumvetsa zimene Yesu adanena. Kawirikawiri masiku amenewo anthu anali kuganiza kuti ana anali wosafunikira.

'Muyenera kusintha ndi kukhala monga tiwana iti', Yesu adawawuza (Mateyu 18:3). Ngati simutembenuka, nimukhala monga tianato simungathe kulowa ufumu wa kumwamba. Chifukwa chake aliyense amene adzichepetsa yekha monga kamwana aka yemweyo ali wopambana mu ufumu wa kumwamba (Mateyu 18:4).

Mulungu amakonda tiana. Pakuti ufumu wa kumwamba uli wa totere. Mchifukwa chake Yesu anatiyangata natidalitsa ndi kuika manja pa ake pa ito nalamula kuti ophunzira ake asatiletse.

‘Ngati simutero, simudzatha kulowa mu Ufumu wa Kumwamba. Aliyense amene salandira Ufumu wa Mulungu monga kamwana sakhoza kulowamo’ (Marko 10:15). Iye adawanyamula ana, nawasanjika manja, kuwadalitsa (10:16).

Kuli kwapafupi kwa mwana kudalira. Mwana amakhulupirira ndi kudalira mawu a Yesu mofulumira. Ufumu wa Mulungu wapangidwa ndi wanthu amene amakhulupirira ndi kudalira mawu a Yesu mofulumira.Ufumu wa Mulungu wapangidwa ndi anthu amene amakhulupirira ndi kudalira, monga m’mene achitira mwana wamng’ono.

Tiyenera kulemekeza ndi kuwalandira iwo amene adalira pa Yesu. Ngakhale amene chikhulupiriro chawo chiri chalula ngati cha mwana.

Chiphunzitso cha Yesu chimatanthawuza zinthu izi:

- Tikafuna kukhala wopambana, tidzikhazike tokha kumapeto kwa onse.
- Tikafuna kukhala wopambana, titumikire ena.

Kuti tikhale wamkulu, tikuyenra kudzichepetsa ndikukhala monga kamwana mwachikhulupilro (9:37).

Yesu anapita nalimbikitsa umodzi pakati pawanthu ngakhale pakati pa wotsutsana naye, Pakuti iye wosatsutsana ndi Ife athandizana nafe (9:40). Tikuyenera kupeza njira zabwino zothandizana nawo akutsutsana nafe (9:41).

**Kambiranani:**

1. Kodi Yesu adawafunsiranji Akuphunzira Ake pa zomwe anali kukangana (9:33)?
2. Kodi Yesu adanenanji za wofuna kukhala woyamba(9:35)? Kodi asowekanso kutiwuza ife zomwezo?
3. Kodi Yesu adanenanji zokhudza ana ang’ono (9:37; Mateyu 18:1-5) Kuli koyenera bwanji kuti ife tikhale monga enawo?
4. Kodi titha kumulandira bwanji Yesu (9:37)?
5. Ndi anthu amtundu wotani amene Mulungu adzawalandira mu Ufumu Wake?
6. Yesu adawaphunzitsa chiyani Akuphunzira Ake pa zakukhala wamkulu?
7. Ndi chifukwa chiyani Yesu adanena za chikho cha madzi (9:41)?

## Werengani Marko 9:42-50

## CHOTSANI UCHIMO MMOYO WANU

Yesu anachenjeza kuti tisawatsogolere ana ku uchimo (9:42). Adatinso tisawanzunze, kuwavutitsa ndi kuwasowetsa mtendere ngakhale kuwachita zoyipa.

Yesu sadafune kuti ife ‘tiduledi manja athu’ (v. 43) kapenanso ‘kuduladi phazi lathu’ (v. 45) ngakhalenso kuti ‘tikolowoledi diso lathu’ (v. 47) ayi. Kutero sikudzatiletsa ife kuchimwa, kapena kumupanga Mulungu kutikhululukira machimo athu ayi. Yesu anali kufuna kuti ife tidziwe kuti kuli kowopsya kuti ena achimwe chifukwa cha ife (v. 42). Kutero kukhoza kutibweretsera chilango ndi

mkwiyo wosatha. Mphero ndi yolemera kwambiri, mwala wokhala ndi mphako pakati pamene anali kuperapo ngala kuti zikhale ufa.

Yesu anali kunena pamenepa za chilango (gehena). Ngati simukhulupirira za chilango, ndiye kuti simukhulupirira Baibulo. M'neneri Yesaya ananena za ng'anjo monga chiweruzo cha Mulungu (Yesaya 66:24) Yesu adagwiritsa ntchito uthenga wa mneneriyu (Marko 9:48).

Anthu anadziwa zimene Iye anali kunena. Iwo anali kutaya zinyalala zawo kunja kwa mzinda Izi zinadzala mu chigwa chonse. Moto umene unali kuyaka kumeneko ndipo malowo anali wodzaza ndi ntchentche ndi mbozi (nyongolotsi/mphutsi). Yesu ananena izi kuti asonyeze m'mene gehena iti idzakhalire.

M'malo mwake, Yesu ananena kuti tiyenera kukhala ofunikira monga mchere. Kenaka Iye adaphunzitsanso china chake chofunika (9:50).

'Tikhalirane mwa mtendere wina ndi mzake'.

## 📖 Werengani: Marko 10:1-12

## ZOKHUDZA KULEKANA PAKATI PA MAMUNA NDI MKAZI

Aphunzitsi a lamulo la Chiyuda anafunsa Yesu kuti: 'Kodi ndi koyenera kuti mamuna asiye mkazi wake?' (10:2). Kulekana kunali kufala, koma lamulo la Mulungu linali kunenanji pa nkhaniyi? Mose anali kulola mamuna kutenga kalata ya chilekaniro ndi kuchotsa mkazi wake (Deuteronomo 24:1-4).

Yesu anawawuza kuti: 'Mose analemba lamulo limeneri chifukwa cha kuwuma mtima kwanu: Kodi simunawerenga?' Iye adawafunsa ndi kuwawuza za lamulo la Mulungu lokhudza ukwati (10:7; lochokera pa Genesis 2:24).

Mulungu amafuna kuti mamuna m'modzi akhale naye mkazi m'modzi, mpaka imfa. Ichi ndiye chinali cholinga chake.

Adamu ndi Hava anachimwa ndi kusokoneza chikonzero cha Mulunguchi. Tchimo limapatsa anthu dyera ndi nkhanza. Ife monga ochimwa sitingathekukonda ena kotheratu chifukwa timadzikonda kwambiri. Choncho pamene mamuna akwiya ndi mkazi wake, nthawi zina amasudzula mkaziyo. Yesu anati sizinali chomwecho pa chiyambi (Mateyu 19:9).




**Jesus abençoa as mulheres e seus filhos pequenos**

### Kugonana; Ukwati; Kulekana

Mulungu adapanga lamulo limodzi lokha la ukwati. 'Mwamuna adzasiya atate ake ndi amake nadzaphatikana ndi mkazi wake. Awiriwa ndipo adzakhala thupi limodzi' (Genesis 2:24). Lamulo lokondweretsa kwambiri. Amuna atati asunge lamulo la Mulungu la ukwatili, mavuto ambiri am'banja sangakhalepo.

Mulungu adadziwa kusoweka kwa mkazi kwa munthu wa mamuna. Iye adadziwanso kuti ana adzasoweka atate ndi amayi. Lamuloli limateteza ukwati pakati pa mamuna ndi mkazi ndiponso kutchinjiriza banja lonse.

Chotero, chiri chikonzero cha Mulungu kuti mamuna ndi mkazi abwere pamodzi mu chiringanizo cha ukwati. Ndi mbali ya chikonzero cha Mulungu kuti awiriwa akhale ndi ana pamene akwatirana.

Anapanga kukhala chosangalatsa kugonana kuti athe kukhala ndi ana. Kugonana kukadakhala kosakoma bwenzi kulibe ana choncho chilengedwe cha Mulungu chikadatha.

Koma ife tikafuna chimwemwe chogonana tisanalowe m'manja pamenepo tichimwira chilinganizo cha Mulungu. Mamuna ndi mkazi akasangalala ndi kugonana, kenaka ndi kupha moyo wosabadwawo potaya mimba, achimwira chikonzero cha Mulungu chokhudza ana. Tikakhala ndi ana tisanalowe m'manja, pamatha kukhala mavuto ndi kusowa chisangalalo kwa anawo.

Tikatinso tipeze njira zina zosangalatsira matupi athu tikulakwiranso chikonzero cha Mulungu. Munthu akakhala ndi akazi oposa m'modzi zimabweretsa nsanje ndi kukhumudwa. Ngatinso mamuna asiya mkazi wake ndikutenga wina, pamakhala mkwiyo ndi kuwawidwa mtima.Yesu adadziwa kuti chinali chikonzero cha Mulungu kuti mwamuna akhale wokhulupirika kwa mkazi m'modzi m'moyo wake wonse ndi kuti asakhale naye wina wapambali. Munjira imeneyi ana akhoza kubadwa ndi kukula mu banja lachikondi mosakhumudwitsidwa ndi kusakhulupirika kwa makolo awo. Yesu anati ichi ndicho chikonzero cha Mulungu kuyambira pachiyambi. (Mateyu 19:8)

Dziwaninso kuti ngati m'manja mulibe ana, sindiye kuti palibe ukwati ayi. Banja ndi anthu awiri. Ana sakutchulidwa mu Genesis chaputala 2. Choncho ndi kulakwa kuthetsa ukwati chifukwa choti sitikubereka ana. Ndi kulakwanso kuwumiriza mabanja kuti akhale ndi ana. Ukwati ndi wodzaza ngakhale palibe ana. Kutenga ndi kulera ana wovutika chingakhale chinthu chabwino kwa mabanja wopanda ana. Ndi kulakwitsanso kunena kuti aliyense ayenera kukwatira. Yesu adati anthu ena adzatumikira Mulungu pokhala wosakwatira ndiponso kusala zogonana ndi kubereka ana (Mateyu 19:11-12).

Motero ukwati pakati pa mamuna ndi mkazi ndi chikonzero cha Mulungu ndipo kulekana ukwati ndi nzeru ya munthu (19:8). Lamulo la Mulungu silingathe kusinthidwa pondanda wina kumva zowawa. Choncho kulekana ukwati ngakhalenso kugonana anthu asanalowe m'manja ndi zolakwika.

Amuna sayenera kuwumiriza akazi awo kuti agonane nawo. Izi ziyenera kuchitika mwa chikondi chochoka pansi pa mtima monga mwa mawu a Mulungu. (Nyimbo Ya Solomo) Kusamvera malamulo a Mulungu pa zakukhala pamodzi kwa mamuna ndi mkazi kutha kubweretsa imfa ya msanga, osati moyo chifukwa cha kachirombo ka HIV ndi matenda a AIDS. Miyoyo yathu imawonongeka munjira zambiri ngati malamulo a Mulungu pa za ukwati, kugonana ndikusiyana ukwati satsatidwa. Ngati chisangalalo chathu pakati pa mamuna ndi mkazi ziri zolakwika titha kuputa mkwiyo wa Mulungu ndi kulangidwa (Genesis 19).

Pamene chikondi cha Mulungu chilamulira mu mitima ya anthu (amuna) iwo amatha kumvetsa kuti Mulungu amafuna kuti ukwati ukhale wosatha mpaka moyo wonse wa munthu. Ukwati ndi kulunzanitsidwa kwa mamuna ndi mkazi mpaka miyoyo yawo yonse.

Mu Marko 10:11, Yesu anati kulekana kuti wina akakwatirenso kwina ndi chigololo. Iye anati ukwati ukhoza kutha ngati m’modzi wa awiriwo apezeka ndi tchimo la chigololo (kusakhulupirika) (Mateyu 19:9).Pa nthawi imene Yesu anali pa dziko pano amuna anali kuganiza kuti akazi ndi ana sanali ofunikira kwenikweni. Koma Yesu anawawonetsa mu uthenga Wake ndiponso m’mene anali kuchitira ndi amayi ndi ana (Marko 10:9; 12:43; 14:6; 9:36, 10:14).

## Werengani: Marko 10:17-31

## M’MYAMATA MWINI CHUMA CHAMBIRI

Wachinyamata wina, Maulamuliro’ (Luka 18:18) anamuthamangira Yesu nanena ‘Mphunzitsi wabwino, ndichite chiyani kuti ndilandire moyo wosatha?’ (Mateyu 19:16).

Anali munthu wabwino komabe anali kumva kuti anayenera kuchitapo kanthu kena kuti akalowe mu Ufumu wa Mulungu. Anthu ambiri timamva chimodzimodzi. Munthu uyu analikusunga malamulo a Mose, koma Yesu anaona kuti anasowabe kanthu kena. Ngakhale anali kusunga chilamulo iyeyu sanathe kukonda anzake ngakhale kusamalira wosowa.

‘Chinthu chimodzi chikusowa’, Yesu ananena naye. ‘Pita, ukagulitse zonse uli nazo ndi kupereka kwa wosowa mawu awa anamukhumudwitsa mnyamatayu. Iye anakonda ndalama ndi katundu wake koposa. Kunali kovuta kulekana nacho chuma chake. Ndi nkhope yachisoni anangochokapo.

Anthu ambiri amatsogoza chuma chawo mu miyoyo yawo. Izi zimawalepheretsa kutsatira Yesu monga Ambuye ndi Mpulumutsi wawo (Mateyu 6:21, 33; Yakobo 5:3).

Akuphunzira anadabwa ndi mawu a Yesu nafunsana wina ndi mzake kuti: ‘Angathe kupulumuka ndiye ndani?’ (10:26)

‘Zonse ndi zotheka ndi Mulunguu’, Yesu anawayankha (10:27). atha kupulumutsa ngakhale achuma ngati iwowo angadalire ndi kumvera Iye. Yesu

anali atawawuzanso kuti wotsatira enieni a Ufumuwo ayenera kusiya njira zawo za dyera ndi kumutumikira Ambuye (8:34). Mulungu adzawapatsa zinthu zoposa zimene iwo angalekane nazo. Komanso ayenera kukonzekera kukumana ndi zowawa.

Kenaka Yesu adawaphunzitsa za Ufumu wa Mulungu (10:31): 'Ambiri apatsogolo adzakhala apambuyo ndi apambuyo adzakhala apatsogolo'.

**Kambiranani**

1. Ngati tikonda kanthu kena koposa Yesu, sitingathe kumukonda Yesuyo kotheratu. Kodi tingawonetse bwanji kuti timukonda Yesu koposa zinthu zina?
2. Kodi mnyamata wachumayu anali wabwino? Perekani zifukwa pa yankho lanu.
3. Ndi chifukwa chiyani Yesu adamuwuza wachumayu kuti akagulitse zonse anali nazo? (10:21)
4. Kodi chinali choposa kusunga malamulo a Mose ndi chiyani?
5. Kodi Yesu adamufunsa wachumayu kuchita zinthu zitatu ziti? (10:21)
6. Tayerekezani zimene Yesu adanena mu Marko 8:35 ndi pa 10:31.

## Werengani: Marko 10:32-45

## MAVUTO AMUTSATA YESU

Tsopano nthawi inafika yakuti Yesu apite ku Yerusalemu kwa nthawi yotsiriza. Iye anafuna kukachita chifuniro cha Atate Wake wa Kumwamba m'malo mothawa masawutso amene anali patsogolo pake. Sanabisale pamene anafika mu Yerusalemu (11:9) Pamene anali kuyenda anawawuza anthu kuti Iye adzaphedwa ndipo adzaukanso kwa akufa kupita kumoyo wosatha. Panthawiyi adanenanso zambiri zokhudza imfa Yake. Adawawuza Akuphunzira ake kuti adzakhalanso ndi moyo patapita masiku atatu.

Akuphunzira adayamba kuchita mantha. Sanafune kuti Mbuye wawo akaphedwe. Mafunso ambiri adawafikira m'malingaliro awo:

- Ndi ndani ati adzamupereke Yesu?
- Ndi ndani ati adzamuyike m'manja mwa akulu ansembe?
- Ndi ndani ati adzalamule kuti Yesu aphedwe?
- Ndi ndani ati adzamuphe?

Kodi mungathe kuyankha mafunso amenewa?

Yesu adatsogolera njira mopanda mantha (10:32). Iye sanawope kupita ku Yerusalemu. Iye adadziwa kuti akulu ansembe ndi ena akamupha, koma ichi chinali chikonzero cha Atate Ake. Iye adafuna kutsiriza ntchito Yake (Yohane 4:34; 5:36; 9:4).

Koma zikuwoneka kuti Akuphunzira Ake sanakhulupirire kuti Yesu adzaphedwa. Anali ndi chikhulupiriro kuti Iye adzakhazikitsa ufumu Wake pa dziko pa nthawi imeneyi.

Yakobo ndi Yohane adafunitsitsa kudzakhala ndi malo awulemu mu ufumu umenewo pamene Iye adzakhala pampando wa ulamuliro. Mayi wa iwowa adafuna kumufunsa Yesu zimenezi (Mateyu 20:20-21).

'Tikufuna, tikufuna', iwo adamuwuza Yesu koma mawu awo adasemphana ndi zonse zimene Yesu anali kuwaphunzitsa.

'Simukudziwa kuti mukupempha chiyani', Yesu adawawuza. 'Kodi mukhoza kumwera chikho cha masautso anga?' (Marko 10:38). Yesu anali kutanthawuza kuti Iye wasankha njira ya manzunzo. 'Kodi mungathe kubatizidwa ubatizo umodzimodzi ndi ine?' Yesu anali kupita kokafa imfa ya pa mtanda. Uwu unali monga ubatizo wa zowawa ndi imfa. Yesu anali kutanthawuza kuti Iye akamizidwa mu ululu ndi kunzunzidwa chifukwa cha machimo a dziko la pansi.

## MTUMIKI WOVUTIDWA

'Mudzanzunzidwa', Yesu adawawuza akuphunzira Ake. 'Koma kudzakhala kudzanja langa lamanja kapena lamanzere si kwa ine kunena ayi', (10:40). Atate adakonza kale kumwamba monganso pansi pano. Ife tiyenera kukhulupirira kuti malo athu alipo. (Yohane 14:2-3; 1 Petro 1:4-5).

Iwo amene amafunitsitsa ndi kuyesetsa atakhala woyambirira, amabwezera ena pambuyo. Amasonyeza dyera, kudziyenereza, ndiponso satumikira ena. Yesu adanena za atsogoleri adzikowa. Amalamulira anthu ndi kuwawuza zochita (10:42). Anthu amayesetsa kupeza njira zolamulira nazo anzawo kuti iwo akhale wopambana. Yesu anati: 'Zisatero ndi inu. Penyani moyo Wanga. Ndinadza kudzatumikira ndi kupereka moyo Wanga. Muyenera kuchita chimodzimodzi' (Yohane 13:4-17).

Yesu anadza kudzatumikira anthu, komanso, kudzafa m'malo mwawo kuti machimo awo akakhululukidwe (1Timothy 2:6). Chikonzero cha Mulungu chinali chakuti Yesu akafe chifukwa cha machimo a ena. Anapereka moyo Wake chifukwa cha machimo amene ife tidachita kuti ife tikapulumutsidwe ndikukhala nawo moyo wosatha ndi Iye kumwamba. Yesu ndiye Mtumiki Wovutidwa. Mulungu ananena za Iye zaka zambirimbiri zam'mbuyomo mwa mneneriYesaya (Yesaya 53:3-6). Ngati tifuna kumutsatira, tiyenera kukonzekera kusiya zambiri ndiponso kukumana ndi mavuto (Afilipi 2:5-8).

### Kambiranani

1. Ndi chifukwa chiyani Yesu adakwerabe kupita kumzindawo pamene anali kudziwa kuti ena sanali kumukonda?
2. Kodi Yesu adalonjeza Akuphunzira Ake chiyani? (10:29-30)
3. 'Kodi mungathe kuvutika monga ine?', Iye adawafunsa Akuphunzira Ake (10:38). Kodi chidavuta ndi yankho lawo chinali chiyani? (10:39)

## 📖 Werengani: Marko 10:46-52

## YESU ACHIRITSA MUNTHU WA CHIKHULUPIRIRO

Khamu lalikulu linamutsatira Yesu. Atayandikira ku Yeriko anamva munthu akukuwa kuti 'Yesu, Mwana wa Davide, chitireni chifundo ine!' Anthu wopemphapempha anali kupezeka ambiri mu zipata za m'mizinda. Bartimeyu wakhungu anamutchula Yesu kuti ndi 'mwana wa Davide'. Iye adadziwa kuti Yesu anali Mesiya wolonjezedwa, mbadwa ya fuko la Davide! (10:47).

Yesu anamuyankha nati, 'Pita, chikhulupiriro chako chakuchiritsa iwe' (10:52).

Yesu anadziwa kuti Bartimeyu anali ndi chikhulupiriro. Ngakhale mkati mwa khamu la anthu Yesu amamva mapemphero ndi kulira kwa anthu wokhulupirira. Chikhulupiriro mwa Yesu zikutanthawuza kumudalira kotheratu. Sitingathe kumunamiza Mulungu. Iye amadziwa pamene talapadi machimo athu. Amadziwanso ngati tikhulupirira kapena ayi (Aheberi 4:13).


Tikakhala nacho chikhulupiriro, tiyenera kuchitapo kanthu. Pamene tiyankhidwa mapemphero athu pamenepo tidziwa woyankhayo ndi Mulungu.

Apa tikutha kuwona chiphunzitso cha Yesu: Khulupirira Yesu (v.47) chikhulupiriro cha ntchito (v.50) chimayankha pemphero (v.52).

## 📖 Werengani: Marko 11:1-19

## YESU ALOWA MU YERUSALEMU ATAKWERA PA BULU

Patatsala sabata imodzi kuti Yesu akapachikidwe, Iye anakwera napita ku Yerusalemu. ku Betaniya, mudzi wapafupi ndi phiri la Azitona, Iye anatuma awiri a kkuphunzira ake kuti atsogole. 'Mukapeza bulu womangidwa mukamumasule ndi kubwera naye', Iye anawalamulira. Bulu ndi chiweto chimene amachigwiritsa ntchito yonyamula katundu wolemera. Nthawi zina anthu wosawuka anali kukwera pa bulu. Anthu wotchuka ndi wolemera anali kukwera Ngamila (mahatchi). Koma Mulungu anali atanena kupyolera mwa mneneri kuti Mesiya adzabwera atakwera pa bulu wonyozeka (Zekariya 9:9). Izi zinanenedwa zaka mazanamazana Yesu asadakwere buluyo.



**Jesus, montado num jumento, é recebido pela multidão em Jerusalém**

Chotero Yesu adalowa mu mzindawo atakwera pa bulu. Khamulo lidadziwa kumasulira kwa zimenezi. Anthu ambiri adakumana naye ali ndi makhwatha amitengo ndi akanjedza m'manja mwawo akuyimba 'osana!' (Pulumutsa tsopano!) (Yohane 12:13). 'Osana, Wolemekezeka Iye wakudza mdzina la Ambuye! Wolemekezeka Ufumu ulinkudza, wa atate wathu Davide; Hosana m'mumwambamwamba!' (Masalimo 118:26).

Zonse zimene aneneri ananera za Yesu zinakwaniritsidwa (Mateyu 21:5). Zaka zakudikira zidafika pamapeto. Anthu a mu Yerusalemu anamuwona Mesiya. Yesu sanali wandale ayi. Adalowa mu mzindawu modzichepetsa ndi mwamtendere. Sanakwere pa ngamira (hatchi) monga mfumu yokhala ndi asilikali ayi, koma anakwera pa bulu monga chizindikiro cha mtendere.

Yesu akudza m'mitima yathu mu njira yomweyo. Sakakamiza kulowamo, koma agogoda mofatsa. Akudikira ife timutsekulire mitima yathu kuti Iye alowemo (Chivumbulutso 3:20) Kwezani mawu anu ndi kunena 'Hosana!'.

Yesu anapita ku kachisi, malo amene anthu ambiri amasonkhanako mu Yerusalemumo kudzapembedza Mulungu. Anangoyang'anayang'ana osanenapo kanthu popeza kunali kutada. Nthawi zingapo zimene Yesu analowa mkachisi wa ku Yerusalemuyo anali kukhumudwa ndi malonda amene anali kuchitika mu nyumba ya Mulunguyi. Nthawi inakwana tsopano yakuti achitepo kanthu kukonza zimene zinali kulakwika mnyumba ya Atate Wake.

**Kambiranani**

1. Ndi chifukwa chiyani Yesu analowa mu Yerusalemu pa bulu?
2. Ndi chifukwa chiyani Yesu adafuna kuti aliyense adziwe kuti wafika mu Yerusalemu?
3. Ndi zinthu ziti mu mpingo lero zimene zimamukwiyitsa Yesu?
4. Kodi takonzeka kudzudzula ndi kukonza zolakwika ngakhale zingatanthawuze kutaya abwenzi, ntchito yathu, ndi moyo wathu? (Ngati takonzeka tiyeni tichite mwa chikondi mu mitima yathu).

## Werengani: Marko 11:20-33

## CHIPEMBEDZO CHOPANDA PHINDU

Yesu ndi Akuphunzira Ake adakhala ndi Mariya ndi Marita (11:11) ku Betaniya, mudzi wa pa fupi ndi Yerusalemu.

M'mawa wotsatira Yesu adawona mtengo wa mkuyu womera mbali mwa njira. Sanapezapo chipatso, koma masamba okha choncho adati kwa mtengowo: 'Munthu sadzadya zipatso zako nthawi zonse' (11:14).

Yesu analowa mu kachisi. Zimene anawona mu kachisimo zinamukwiyitsa. Mu mabwalo a kachisiyo anthu anali kugulitsa ng'ombe, nkhosa ndi nkhunda zoperekera nsembe. Ena anali atakhala pa magome kusinthanitsa ndalama za Chiroma ndi za Kachisi. Anali atasandutsa nyumba ya Mulunguyi msika. Ayuda anali kupanga phindu lalikulu ndi zimenezi.

Yesu anawapirikitsa onse amene anali kuchita malonda mu Kachisiyu ndi kugadabuza magome a wosinthitsa ndalama.

'Kodi sikudalembedwa kuti nyumba yanga idzatchedwa yopembedzeramo amitindu yonse? Koma inu mwayisandutsa phanga la achifwamba' (11:17; Yesaya 56:7)

Atsogoleri a Chiyuda anali kupembedza modziwonetsera, koma mitima yawo inali yowuma ndi yopanda kanthu. Anali ngati mtengo wa mkuyu uja, wopanda chipatso koma masamba wokha. Miyoyo yawo sinathe kumusangalatsa Yehova.

Pambuyo pake akuphunzira adawona mtengo wa mkuyu uja. Masamba ake anali atawuma ndi kuyoyoka (11:20). Anadabwa nati kwa Yesu, 'Mphunzitsi, tawonani! Mtengo munawutemberera uja wauma'.

**Kambiranani**

1. Chinachitika ndi chiyani kwa mtengo wa mkuyu (Mateyu 21:19).
2. Kodi moyo wanu uli ngati mtengo wokhala ndi masamba okha kapena wokhala ndi zipatso?
3. Kodi Yesu atafika pa mpingo panu lero angapeze zotani? Angapeze mapemphero, kutamanda ndi nsembe? Kapena angapeze miyoyo yotanganidwa yopanda Mulungu — chipembedzo chopanda phindu?

## KHULUPILIRANI MULUNGU

'Mukhale ndi chikhulupiliro mwa Mulungu,' akunena Ambuye Yesu (11:22). Chikhulupiliro chilli ndi mphamvu yosutha mapiri. Izi zikutitsimikizira kunena kuti chilichotse choima patsogolo pathu chotsutstsana ndi chifuniro cha Mulungu; Munthu akakhala akakhulupilira Mulungu chimachoka. (11:23).

Yesu adaphunzitsa anthu mu kachisi. Ansembe ndi akuluakulu ena anakwiya. Iwo sanafune kuti Iye akhale mu kachisi wawo. Anali atapirikitsa anthu amalonda ndiponso anali kulola ana kumakuwa 'Hosana kwa Mwana wa Davide' (Mateyu 21:15).

Apa nkuti patangotsala masiku pang'ono kuti Yesu akapachikidwe. Tiyeni tiphunzire mwachidwi zimene Yesu adawaphunzitsa otsatira Ake pa nthawi imeneyi. Iye adawawonetsa kuti ayenera kukhala ndi chikhulupiriro chakuya ponena kuti:' Musamakayika mu mtima mwanu. Muzikhulupirira kuti zimene munena zichitika. Mukatero Mulungu adzikuchitirani' (11:23). Ndiye adanenanso kuti: 'Mukapemphera ndi kukhululukira aliyense amene ali nanu mangawa, Atate wanu wa Kumwamba azikukhululukiraninso inuyo' (11:25, 26).

MuKachisimo ansembe akulu ndi alembi adamufunsa Yesu kuti anali kuphunzitsa ndi ulamuliro wotani? Poyankha Iye adawafunsa kuti kodi ubatizo wa Yohane udachokera Kumwamba kapena kwa anthu?' (11:30). Kodi iwo adayankha kuti chiyani? (11:33)

Atsogoleri achipembedzowa sanali kudziwa kwenikweni kuti Yohane M'batizi anali ndani. Sanali kudziwanso kuti Yesu anali ndani. Iwo sanadziwe popeza

sanamvetsetsa chowonadi cha Mulungu. Sanamvetse zolembedwa zopatulika zonena za Yohane ndiponso Yesu. Sanazikhulupirira izo.

Leronso alipo anthu ambiri amene satha kumvetsetsa zinthu za Mulungu pamene zifotokozedwa kwa iwo. Salandira chowonadi ndipo safuna kuchikhulupirira. Chowonadi chinalembedwa mu Baibulo kuti aliyense athe kuwerenga ndi kumvetsetsa. Koma anthu ambiri sakhulupirira Mulungu. Iwo samvetsetsa kuti Yesu adafa kuti machimo awo akakhululukidwe. Amakhala moyo wa umbuli ndipo afikira kufa wopanda chikhululukiro cha Mulungu. Motero iwo sadzatha kupita Kumwamba kukakhala ndi Yesu.

Ife tiyenera kuthandiza anthu kuti amvetsetse chowonadi cha Mulungu pamene akadali ndi moyo. Yesu adatilonjeza ife kuti Mzimu Woyera adzatithandiza kumvetsetsa ndi kuti tithe kuphunzitsa ena za chowonadichi (Yohane 15:26; 16:13-14).

## 🕮 Werengani: Marko 12:1-11 (werenganinso Mateyu 21:33-46)

## FANIZO LA WOSUNGIRA MUNDA

Patatsala masiku atatu wokha kuti Iye akapachikidwe, Yesu ananena nthano ya mwini munda. Eni minda anali kulola anthu ena kumalima minda yawo.

Mwini munda uyu adalima munda wake wa mphesa nawuzunguliza ndi linga (mpanda) kuwopetsa ziweto. Anakumbanso malo wopsyinyira mphesa. Awa ndi malo amene amaponderapo mphesazo ndi kupsyinya madzi ake. Anamanganso nsanja ya alonda woyang nira mundawo kuwopetsa akuba. Potsiriza adapeza anthu wogwiramo ntchito mu mundawu.

Itafika nthawi yokolola iye anatuma atumiki ake kuti akatenge zipatso za mphesa ndi madzi a zimene adapsyinya. Koma antchito aja adawamenya wotumidwawo nawabweza wopanda kanthu. Ena mwa atumikiwa adawapha. (12:5)

Mwini munda adatsala ndi munthu m'modzi yekha amene akadamutuma. Uyu ndiye mwana wake amene adamukonda. Iye adaganiza kuti mwanayo akamulemekeza. (12:6).

Antchito aja atawona mwanayo akudza potero anati: mwana wa mwini munda akubwera. Tiyeni timuphe ndipo zonse zidzakhala zathu. Iwo adagwira mwanayo ndi kumupha (12:8).

Yesu adanena fanizoli makamaka kwa atsogoleri a Israeli amene anali kukonza zomupha Iye. Anawuza ndi cholinga chowachenjeza. Mulungu adatumiza atumiki Ake amene anali Aneneri kuti akawayankhule koma iwo sanawamvere. Anatumiza Aneneri ena koma awanso adawachita chipongwe (Luka 11:48). Yohane M'batizi atatumidwa adaphedwa. Kenaka Mulungu adatumiza Mwana Wake Yekhayo, Yesu Khristu. Uyunso adamupha (Yesaya 53:10).

Fanizoli likupereka chithunzi cha m’mene Yesu ati adzafere- Iye adzaphedwa ndi anthu amene sanafune kumulandira ngati Mwana Wa Mulungu. Momwemonso sadathe kuwalandira ena amene Mulungu adawatuma.

Fanizoli likuperekanso chithunzi cha m’mene mpingo uliri lero. Mpingo ndi wa Mulungu osati anthu ayi. Iye amafuna kuti ubale chipatso. Mulungu amawutchinjiriza kwa adani Ake, ndipo adawusiya m’manja mwa antchito Ake kuti alime ndi kukolola zambiri. Koma antchito ena amafuna kuti zonse zikhale zawo. Samatha kupereka chopereka kapena kumuthokoza mwini munda. Mwini munda amamumvetsa chisoni ndi kumukwiyitsa.

Mulungu amafuna anthu Ake azimukonda ndi kumuyamika ndi mitima yokondwa (Aheberi 13:15).

## ATSOGOLERI ACHIPEMBEDZO AYESA KUMUPEZERA ZIFUKWA

Akulu ansembe atamva Yesu akunena fanizoli, adafuna njira yoti amukole nayo. Iwo adadziwa kuti Yesu anali kunena za iwowo mu fanizoli.

Iye adati kwa iwo ‘Kodi simunawerenga zimene malemba anena kuti: mwala umene amisiri womanga nyumba adawukana womwewo udayesedwa mwala wa pa ngodya Ichi chinachokera kwa Ambuye, ndipo chiri chozizwitsa m’maso mwanu?’ (Masalimo 118:22-23).

Mavesi a zolembedwa zina za mu Chipangano Chakale amapezekanso mu Chipangano Chatsopano (Yesaya 28:16; Machitidwe 4:11). Mu uthenga wa Marko wokhawu muli mavesi woposa makumi asanu wochokera mu Chipangano Chakale. Mu uthenga wa Mateyu muli mavesi pafupifupi makumi asanu ndi anayi (90) opezekanso mu Chipangano Chakale. mwala wofunikira kwambiri’ ndi woyambirira kukhazikitsidwa pomanga nyumba yatsopano. Mwalawu umapezeka pa ngodya ya makoma awiri, pamene nyumba yonse imadzayeramirapo. Nyumba ya Mulungu, Mpingo Wake, uyedzamira pa Yesu. Iye ndi amene alunzanitsa zonse. Yesu ndi mwala wa pa ngodya pa mpingo (Aefeso 2:21-22). Yesu adadziwa tanthawuzo la Uthenga wa mu Masalimo 118 ndipo adadziwa kuti uthengawu udzakwaniritsidwa posachedwa mwa Iye.

Yesu adanena zinthu izi kwa Akulu ansembe ndi atsogoleri ena achipembedzo. Iwo sanawukonde mwambi umenewu, ngakhalenso m’mene Iye amamasulira zolembedwa zopatulikazi. Iwo adadziwa kuti anali kuwadzudzula, choncho adayamba kumukonzera chiwembu chofuna kumugwira. Adamufunsa Yesu kuti anali kuyankhula ndi ulamuliro wa yani (11:28). Iwo sanadziwe ndi kukhulupirira kuti Mulungu adamupatsa Yesu ulamuliro.

Mulungu adaweruza onse amene adamupha Yesu. Zitangochitika zimenezi, mu AD 70, mzinda wawowu ndi kachisi yemweyo zidawonongedwa. Komabe kuposera apo nzeru za ambiriwo zinakhalabe zomangika, motero sadzatha kulowa Ufumu wa Mulungu (2 Akorinto 3:14).

Afarisi adafuna kumukola Yesu kupyolera mu mawu ndi mayankho Ake (12:13). Iwo adadziwa kuti anthu sakonda kupereka msonkho kwa Aroma,

choncho adamufunsa maganizo Ake pa mnsonkho. Yesu adadziwa kuti anali kufuna kumukola. Iye akadanena kuti 'Perekani mnsonkho', anthu akadakwiya. Komanso akadati Musapereke mnsonkho'atsogoleriwa akadakamunenera kwa Herod kuti akuletsa anthu kupereka mnsonkho.

Yesu adati; 'Nditengereni lupiya latheka kuti ndiliwone' (12:15). Atamupatsa ndalamayo Yesu adayiyang'ana. Ndalama zambiri zinali zosindikizidwa nkhope ya wolamulira. Ndalama za chi Roma zinali ndi nkhope ya Kaisara.

'Ndi nkhope ya ndani iri apayi?' Yesu adawafunsa. 'Ya Kaisara', iwo adamuyankha.

'Perekani kwa Kaisara zake za Kaisara ndi kwa Mulungu, zake za Mulungu' (12:17) Apa Yesu adawonetsa kuti tikhoza kumvera wolamulira mu njira zambiri popanda kulakwira malamulo a Mulungu.

## Werengani: Marko 12:18-34

## SADZIWA CHOWONADI CHA MULUNGU

Ndipo Asaduki anadza kwa Yesu. Iwowa sanakhulupira kuti kulikuwuka kwa akufa. Anafuna kumyesa Yesu ndi lamulo la Chipangano Chakale. Mungoyerekeza kuti mwamuna wafa, ndiye mkazi wotsalayo ndi kukwatiwanso. Atakhala kuti pamoyo wake wakwatiwa ndi amuna asanu ndi awiri, kodi podzawuka, mkaziyo adzakhala wandani?', iwo anamufunsa Yesu (12:20-23; Deuteronomo 12:19).

Yesu anawawonetsa kulakwitsa kwawo. mudziwa za Zolembedwa zauzimu….Akufa adzawuka, koma adzakhala monga angelo', Yesu anawayankha. M'ngelo sakwatira (12:24-27).

Kenaka adawafunsa kuti: 'kodi simunawerenga? Mulungu anati kwa Mose, 'Ine ndine Mulungu wa Abrahamu, Mulungu wa Isake, ndi Mulungu wa Yakobo'. Iye si Mulungu wa anthu akufa ayi koma amoyo' (Eksodo 3:6). Anthu amenewa ali ndi moyo ngati Mulungu akunena kuti ndi Mulungu wawo. Ziphunzitso zawo zidawatsimikizira kuti kuli moyo wina itapita imfa. Akulu achipembedzowa sadathe kumvetsetsa ziphunzitso zawo. Ife tisakhale ngati iwo. Tiyenera kudziwa Baibulo lathu ndikufunsa chidziwitso cha Mulungu tsiku ndi tsiku.

Atsogoleri azipembedzowa akuwonetsanso kuti sanali kumudziwa Mulungu, chikondi Chake, mphamvu Yake, ndi chowonadi Chake (12:24). Yesu anati iwowa anali anthu woyipa m, mitima yawo (Mateyu 9:4). Anthu woyipawaanali kufuna kuwonetsa kuti Yesu ndi wolakwa. Leronso, alipo anthu amene amanena zoyipa za Yesu. Kuyipa kwa mitima yawo ndi kumene kumawapangitsa kutero. Iwowa amangosonyeza kuti samudziwa ndi kumumvetsetsa Mulungu ndi Mawu Ake opatulika.

## MTSOGOLERI WA CHIPEMBEDZO WODZIWA CHOWONADI CHA MULUNGU

Mphunzitsi wa chilamulo adamva kuyankha kwa Yesuku. Iye adafunsa kuti, kodi pa Malamulo onse (a Mulungu), lamulo lalikulu ndi liti?' (12:28).

Munthuyu analibe cholinga chomukola Yesu. Iye adafuna kudziwa chowonadi. Izi zidamukondweretsa Yesu (12:34). Yesu adamuphunzitsa munthuyo zotsatirazi:

- Ambuye (Yahweh) ndiye Mulungu.
- Ambuye Mulungu ndi m'modzi.
- Konda Mulungu koposa zonse.
- Konda mzako monga udzikonda iwe mwini.

Munthuyo anakhulupirira zinthu zonsezi. Yesu anamuwuza kuti sanali kutali ndi Ufumu wa Mulungu (12:34). Komabe mwina sanadziwe kuti Yesu anali Mwana Wa Mulungu.

**Kambiranani**

1. Kodi ndi chifukwa chiyani atsogoleri a chipembedzo adamufunsa Yesu mafunso (12:13)?
2. Ndi chifukwa chiyani kuli kofunika kumvetsetsa zimene Baibulo linena?
3. Kodi akhristu ayenera kuthangata boma motani? Ndi njira ziti zimene zingakhale zolakwika pa kutha ngata boma?
4. Kodi inu mukuganiza kuti lamulo lalikulu ndi liti (Deuteronomo 6:4, 5)?
5. Kodi Yesu adayankha chiyani pa funso la mphunzitsi uja (12:30, 31)?

## Werengani: Marko 12:35-44

## KODI YESU NDI MWANA WA NDANI?

Zaka zambiri zapitazo, Mfumu Davide adalemba za Mesiya (Khristu) amene adzabwere. Iye adamutchula kuti; mbuye wanga' (Masalimo 110:1). A Yuda anali kudziwa kuti Mesiya-Khristu adzafumira ku m'bado wa Davide, koma iwo anali kuyembekezera mfumu imene iti idzalamulire dziko lapansi.

Yesu anawawuza iwo kuti Iye sanali mbadwa ya fuko la Davide kokha ayi, koma anagwiritsa ntchito mawu wonenedwa ndi Davide powawuza kuti Iye anali Ambuye wa Davide. (Masalimo 110:1) Tsopano ife tidziwa kuti ali wa fuko la Davide komanso kuti ali woposa Davide. Iye ndi Mwana Wa Mulungu. Yesu ndi Mfumu, Mesiya wonenedwa ndi Davide kapena kuti Khristu! Kodi Iyeyu ndi Khristu wa moyo wanunso inuyo?

Anthu adadziwa kuti Yesu sanali ngati aphunzitsi awo amene anali:

- Kukonda kuvala zovala zodziwonetsera;
- Kukonda kupatsidwa moni mu misika;
- Anali kufuna kupatsidwa mipando ndi mawu awulemu;
- Anali kupemphera mapemphero ataliatali modziwonetsera;
- Anali kulanda ndalama za amayi amasiye m'malo mowasamalira.

## PEREKANI KWA MULUNGU MWA CHIKONDI

Mubwalo la kachisi munali malo akuluakulu operekera khumi ndi atatu. Ansembe anali kugwiritsa ntchito ndalama zinali kuyikidwa m'menemo pogulira chakudya, ndi kulipirira wokonza kachisi. Yesu anawona mayi m'modzi wa masiye akubwera ku bwaloli. Amayi ana kuloledwa kufika mpaka pamenepa koma asapitirire. Mayiyu anaponya tindalama take tiwiri mu chotengera chopereka.

Anthu achuma anali kuponya matumba akuluakulu mu zotengerazi. Anali nazo zambiri, motero kunali kosavuta kwa iwo kuperekanso zochuluka. Koma mayi wamasiyeyu adapereka zonse zimene anali nazo (12:44). Izi zinasonyeza m'mene iye anali kumukondera Mulungu wake.

Tikhoza kupereka pang'ono kapenanso zambiri kwa Ambye wathu. Kupereka ndi kosavuta pamene tiri ndi zambiri zoti tikhoza kupereka, koma kupereka zonse zimene tiri nazo ndi kovuta. Ngati timukondadi Mulungu tikhoza kutha kupereka zonse kwa Iye pomupatsa mitima yathu.Tiyeni timupatse mphatso zathu ndi luso lathu Mulungu ndi mitima yokondwera (Eksodo 25:2; 35:21-29).

### Kambiranani

1. Ndi mafunso wotani amene Yesu adawafunsa anthu (12:35)?
2. Kodi Yesu akhala bwanji mbadwa ya Davide komanso ndikukhala Ambuye wake (Mateyu 1:6, 16)?
3. Davide ananena chiyani za Yesu (Masalimo 110:1)?
4. Yesu ananenanji pa mpatso ya mkazi wamasiye (12:43)?
5. Ndi ndani anakonda Mulungu koposa- atsogoleri achipembedzo ndi mayi wa masiye?

## Werengani: Marko 13:1

## YESU APHUNZITSA ZA KUTSOGOLO

Anthu ambiri adafika ku kachisi kudzamvera Yesu akuphunzitsa. (Luka 21:38). Potsiriza Yesu ndi akuphunzira Ake adapita kunja kwa mzinda pa phiri la Azitona. Atayang, ana mbali ina ya chigwacho anawona kuti mzinda wa Yerusalemu unali kuwoneka bwino kwambiri. Akuphunzira analozerana makoma amzindawo moyamikira (13:1).

Yesu adawawuza kuti, 'Sudzasiyidwa pano mwala umodzi pamwamba pa unzake, umene sudzagwetsedwa' (13:2). Izi zinachitika patatha zaka makumi anayi. Anthu akuti golide wa mukachisi atasungunuka ndi moto adalowa muming'alu ya miyala ya khomalo. Izi zidapangitsa asilikali a Chiroma kuchotsa mwala umodzi ndi umodzi kuti apeze golideyo.

Tonse timafuna titadziwa zimene zidzachitike mtsogolo, koma Mulungu amangotiwuza zimene ziri zoyenera ndi zabwino kuti tizidziwe. Mulungu yekha ndiye adziwa zimene zidzachitike kutsogolo. Iye adatiwuza kuti tsiku lina posachedwa Yesu adzabweranso pa dziko lino la mitambo'(Mateyu 24:30).

Nyumba zathu zikuluzikuluzi ndi mabungwe athuwa adzakhalapo kufikira pamene Mulungu adzafune.

## ZINTHU ZIMENE ZIDZACHITIKE

Yesu adawawuza Akuphunzira zina mwa zinthu zimene zidzachitike. Zina mwa izi zinachitika patangopita zaka zochepa, koma zina zinachitika patapita nthawi yayitali. Zambiri za zinthu izi zadachitika kale, ndipo zina zichitika posachedwa. Ife zimenezi sitikuzidziwa.

Yesu anati, 'Yang'anirani kuti munthu asakusocheretseni'.(13:5). Anthu adzaphunzitsa zonama. Ena adzanena kuti ali Khristu. Enanso adzanena kuti akudziwa tsiku limene Yesu ati adzabwerenso kufuna kusokeretsa anthu. Yesu adati, 'musamale ndi wotere' (Mateyu 24:24). Zinthu zazikulu ziwiri zimene zidzachitike ndi:

Kachisi adzagwetsedwa (13:2; Mateyu 24:15)-izi zidachitika patapita zaka – makumi anayi Yesu atanena mawu amenewa.

Yesu adzabweranso mu mphamvu ndi ulemerero (13:26).

## NKHONDO YA AROMA IDZABWERA

Yesu adawawuza Akuphunzira 'Ake kuti, mukadzawona Yerusalemu atazungulidwa ndi asilikali Achiroma, mudzathawire kumapiri' (Luka 21:20-21). Kenaka Iye adanena za chizindikiro. Chizindikiro chimene Yesu adanena (13:14), chingakhale chakuti Aroma adzabweretsa mu Kachisi mafano awo ndi kumuyipitsa. (Luka 21:20).

Mawu a Yesuwa adawathandiza Akuphunzira kukonzekera kugwa kwa Yerusalemu. Adawawuza m'mene ati adzathawire nkhondo ya Aroma. Iwo sanayenera kudikira chozizwa chowapulumutsa kuchokera kwa Mulungu.

'Musadzabwerere kukafunako kanthu', Yesu adachenjeza (13:16).

Mu AD 70, magulu ankhondo Aroma motsogozedwa ndi Tito, anawuzinga mzindawu. Akhristu adakumbukira mawu a Yesu powoloka mtsinje wa Yordani ndi kukabisala cha kum'mawa.

## YESU ADZABWERANSO

Ndipo idzafika nthawi ya manzunzo, yowawitsa (13:24). Izi zikadzachitika, Yesu adzabweranso. Palibe ati adzadziwe nthawi imene izi ziti zidzachitike (13:32, 35).

Mulungu adalenga angelo amene amamutumikira pa zonse zimene Iye amawatuma, koma ngakhale iwowa sadziwa chikonzero cha Mulungu (13:32). Phunzirani ndi mkuyu fanizo lake.(13:28). Zilipo nyengo zina imene timaona Mzimu wa Mulungu umayembekeza dzinja. Ndipo dzinja likafika mzimu wa Mulungu umabeleka zipatso pa mpingo.Pamene zipatso zacha timazindikira kuti Yesu ali pafupi kubweranso kachiwiri.

Mulungu akamaweruza mizinda ndi mafuko, zitikumbutse kuti Yesu akubweranso posachedwa. Zimenezi zimapangitsa anthu kuganiza mwakuya za

Mulungu. Tiyenera kumuwopa Mulungu, amene ndi woweruza wa onse. Ngati sitimulandira Iye m'mitima yathu tidzayima pa mpando Wake wachiweruzo (Mateyu 25:30; Aheberi 10:27).

M'mawu achisoni ndi achikondi Yesu anati, miyamba ndi dziko lapansi zidzachoka koma mawu Anga sadzachoka'(13:3 10.

Akuphunzira mwina adafuna kufunsa kuti 'Mudzabweranso liti Ambuye'. Yesu adangowayankhiratu powawuza fanizo limene likadawathandiza kumvetsetsa (13:34-36). Iye adawawuza fanizoli pofuna kuchenjeza anthu Ake kuti azikhala maso ndi kuyang'anira kubweranso kwake.

'Ndipo chimene ndinena kwa inu ndinena kwa onse, Dikirani' (13:37). Palibe amene adziwa kuti Yesu adzabweranso liti. Yesu adati ngakhale Iye mwini sadziwa (13:32)!

Tikhoza kugwiritsa ntchito nkhani iri pa vesi 34 kutikumbutsa za mpingo kuti:

- Mpingo ndi wa Yesu Khristu.
- Iye amayika womutsatira kuti awulamulire.
- Aliyense ali ndi ntchito yoti ayigwire.

Tiyenera kuyang'anira kubweranso kwa Yesu. Kodi Iye adzatipeza tiri mtulo' pamene abwera (13:36)?

Pamene Yesu akubweranso adzabwera monga Mfumu Yesu! Iye adzabwera ndi angelo a Kumwamba (Mateyu 24:30-31) Panthawi imeneyi angelo adzatenga anthu onse a Mulungu kukakhala ndi Iye kwa nthawi zonse (13:27).

Pali chikhulupiriro chakuti Mesiya adzalowa mu Yerusalemu podzera pa chipata cha kum'mawa, chimene pano chiri chotseka. Ganizoli limachokera mu zolembedwa zopatulika (Ezekieli 44:1-3).

Yesu akutichenjeza ife kuti kudzakhala nkhondo zambiri (13:8), ndi zivomelezi. Kudzakhala njala ndipo anthu adzakumana ndi mavuto ena ambiri (13:9-13). Panthawiyi mthenga wabwino udzalalikidwa kwa anthu onse a padziko lapansi (Mateyu 24:14). M'masiku otsirizawa, kudzakhala aneneri onyenga ambiri (13:22) koma uthenga wabwinowu udzafikira aliyense, ngakhale mafumu. Ambiri otsatira Yesu adzagwidwa ndi kuzengedwa mirandu, koma adzachitira umboni Yesu. Iwowa ayenera kugwira ntchito molimbika ngati kuti Yesu akubwera nthawi ina iri yonse.

**Kambiranani:**

1. Ndi chinthu choyenera kodi kunyadira nyumba ya tchalitchi yathu?
2. Kodi Yesu adati kudzachitika chiyani mu masiku otsiriza (13:8, 9)?
3. Ndi chifukwa chiyani akhristu sayenera kudankhawa ndi zomwe adzanene pamene awatengera ku bwalo la mmirandu (13:11)?
4. Kodi chimayambitsa udani pakati pa makolo, abale ndi alongo nchiyani(13:12, 13)?
5. Chidzachitika ndi chiyani kwa iwo amene sadzataya chikhulupiriro chawo (13:13)?

6. Kodi Yesu adawawuza chiyani Akuphunzira Ake ponena za nthawi ya kubweranso kwake (13:32)?
7. Tingathe bwanji kudikira ndi kukonzekera Kubweranso Kwachiwiri Kwa Yesu? Iye akhoza kufika nthawi ina iri yonse!
8. Kodi ndife okonzeka kudalira Mulungu pamene mavuto abwera? Mukhoza kudalirabe kwa Yesu ngakhale aneneri onyenga atafika mumzinda (m'mudzi) mwanu ndi kunena kuti iwo ndiye Khristu (mesiya)?
9. Kodi muyenera kuchita chiyani podikira kubweranso kwa Yesu?
10. Kodi mneneri wonyenga atafika kwanuko, mudzamudziwa bwanji kuti akunama?
11. Yesu adanena kuti zinthu zadzayipirayipirabe. Lero tiri ndi zinthu zambiri zopangidwa mwamakono, koma mtima wa munthu sunasinthebe. Satana, mkulu wa zoyipa, watanganidwa koposa kale, kuyesa kunyenga ndi kuwononga anthu (Yeremiya 17:9; 1 Petro 5:8).

## Werengani: Marko 14:1-11

# MMENE WINA ANAWONETSERA CHIKONDI CHAKE KWA YESU

Madzulo a tsiku limenero, ku Betaniya, wina adachita chinthu china chosonyeza kuya kwa chikondi chake kwa Yesu. Yesu anali ku nyumba kwa Simoni (Mateyu 26:6). Marita anali kutumikira pokonza chakudya cha madzulo. Lazalo ndi akuphunzira ena anali atangokhala kudikira.

Pamene adayamba kudya, mayi wina anabwera ndi botolo (nsupa) la mafuta wonunkhira kwambiri ndi amtengo wapatali a nardo. Anabenthula pakamwa pa botololo natsanulira mafuta onunkhira bwinowo pa mapazi a Yesu. Mayiyo anali ndi tsitsi lalitali limene adapukutira nalo mafutawo pa mapazi a Yesuwo. Nyumba yonse idadzaza ndi fungo la mafutawo.

Yesu adakondwera ndi zochita za mayiyu koma Yudasi Iskalioti anakwiya nazo. Iye adamudzudzula mayiyo kuti wawononga mafutawo. Yudasi adati akadapeza ndalama zambiri akadagulitsa mafutawo, zimene akadapatsa anthu wosawuka. Komatu sikuti iye anali kuganiza za anthu wosauka ayi. Yudasi anali wakuba. Iyeyu anali wosunga ndi kuyang'anira thumba la gululi, koma anali kuba ndalamazo ndikumagulira zosowa za iye mwini.

Yesu anati, 'Mlekeni, mumuvutiranji? Wandichitira Ine ntchito yabwino' (14:6). Ndipo iye anayankhulapo za anthu osawuka. 'Anthu osawuka muli nawo nthawi zonse, mukhoza kuwathandiza pamene mufuna kutero…(14:7). Koma Ine simudzakhala nane'.

Mayiyu adamudzoza Yesu mafuta onunkhira pamene anali ndi moyo. (Yesu adadziwa kuti posachedwa adzalowa m'manda). Yesu adawawuza amene anali m'nyumbamo kuti chimene adachita mayiyu powonetsa chikondi chake sizidzayiwalika (14:9). Izi zitipatsa ife phunziro: Tiwakonde abale athu pamene tiri nawo. Pamene tiwakonda iwo, tisonyezanso chikondi chathu kwa Yesu. Timutamande Mulungu pamene tidakapuma (Masalimo 150:6).

**Kambiranani:**

1. Kodi mukuganiza kuti mayi uja adadziwa kuti Yesu aphedwa posakhalitsa?
2. .Ndi chifukwa chiyani Yudasi adanena kuti mayiyu wawononga mafuta (14:5)?
3. Yesu adati chiyani pa za wosauka (14:7)? Kodi Iye akufuna kuti tidziwathandiza?
4. Sitingathe kumupatsa mafuta amtengo wapatali Yesu. Kodi Mulungu akutifunsa kupereka chiyani?
5. Kodi Yudasi adakonza zoti Yesu amutani (14:10, 11)?

## Werengani: Marko 14:12-31

## CHAKUDYA CHOTSIRIZA CHA YESU

Zaka zambirimbiri Yesu asadabwere pa dziko, a Israeli adali akapolo mu dziko la Aigupto kwa zaka mazana anayi ndi mphambu makumi atatu. Mulungu mu mphamvu Yake yodabwitsa, adawatulutsa (Masalimo 106:7-11). Pa Paskha iwo anali kukumbukira zimene Mulungu adawachitira. Marko akufotokoza mwambo umenewu.

Banja liri lonse linali kupha nkhosa, monga m'mene anachitira pa Paskha yoyamba ija, mu dziko la Aigupto, pamene mngelo wa imfa adapitirira khomo lawo. Iwo adadya Paskha monga banja. Mabanja a Chiyuda amadyabe chakudya chimenechi chimene amachitchula Sada. Panthawi ya Paskha, anthu anali kuchokera mu madera akutali kubwera ku Yerusalemu.

Yesu anadya Paskha ndi Akuphunzira Ake. Chakudya chimenechi chimadyedwa madzulo-Mgonero. Uwu unali mgonero wotsiriza wa Ambuye. Akhristu kulikonse amakumbukira chakudya chimenechi pakudya mkate ndi kumwa vinyo. Mipingo yambiri imachita mwambowu monga mbali ya kupembedza. Ena amayitchula 'Kunyema mkate' kapena misa kapenanso ukalisitiya. Koma ambiri amawutchula kuti ndi mgonero Wa Ambuye' pokumbukira chakudya chotsiriza chimene Yesu anadya ndi Akuphunzira Ake asanapachikidwe.



**Os discípulos reclinam-se para comer a Última Ceia com Jesus**

Akuphunzira anamufunsa Yesu kuti 'Mufuna tipite kuti ukadyereko Paskha?' (14:12). Yesu anawayankha nati:' Lowani m'mzinda, ndipo adzakumana nanu munthu wakusenza mtsuko wa madzi, mumtsate iye….' (14:13). Kawirikawiri azimayi ndiwo amasenza madzi. Iwo

adamupezadi munthuyo ndipo anawalondolera ku chipinda chapamwamba chimene chinali chokonzedwa kuti akadyeremo Paskha. Chakudyachi chinali chopangidwa ndi nyama ya nkhosa, mkate wopanda chotupitsa, vinyo ndi ndiwo (masamba) zowawa.

Mgonerowu udzawathandiza kukumbukira imfa ya Ambuye wawo, ndi zina zambiri. Adzakumbukiranso kuti zaka zam'mbuyomu, mwazi unali kupakidwa pa mphuthu ya chitseko ku Aigupto (Eksodo 12:7, 13). Pochita zimenezi, mngelo wa imfa anali kupitirira ndipo ana a Israeli anali kupulumuka. Tsono Yesu, 'mkhosa Ya Mulungu' yeniyeni adzaphedwa pa nthawi ya Paskha. Iye anali mwana wankhosa Wa Mulungu amene adzaphedwa. Mwazi Wake unakhetsedwa, kupereka mtengo wa zoyipa zathu (Aheberi 9:12). Imfa Yake iri yopulumutsa anthu onse okhulupirira.

Ali pa gome lodyera, Yesu anawawuza kuti, 'M'modzi wa inu adzandipereka Ine, ndiye wakunsunsa pamodzi ndi Ine m'bale.' (14:18). Yesu anali kutanthawuza kuti adzaperekedwa kwa adani Ake. Aliyense wa Akuphunzira adamufunsa kuti: 'ndine kodi?' (14:19). Yudasi ndiye amene adanupereka Yesu (Mateyu 26:25). Iye atangodya mkate pamodzi nawo, adatuluka kunja (Yohane 13:30).

Yesu anabwerezanso kuti; 'Mwana wa Munthu apita kukaphedwa monga kunalembedwa za Iye' (14:24; Yesaya 53:8-9).

## 'MUNDIKUMBUKIRE INE'

Pamene anali kudya, Yesu anatenga mkate, ndipo pamene anawudalitsa, anawunyema nawupereka kwa Akuphunzira Ake nati: 'muli ndi Thupi Langa lopatsidwa kwa inu'.

Chitani zimenezi kuti mukandikumbukire Ine. Atadya Iye anatenga chikho nati: 'Chikho ichi ndi Chipangano Chatsopano mu mwazi wanga wokhetsedwa chifukwa cha inu'.

Yesu anayitana Akuphunzira Ake ndipo iwo adamutsatira. Iye adawaphunzitsa za Ufumu, komanso anadya nawo mgonero wotsiriza. Anawawuza za kupachikidwa, kuwuka ndi kukwera Kwake kupita Kumwamba. Tsopano anali kudikira kuwona adani Ake akumupha. Iwo adzakumbukira tsiku limeneri la Mgonero monga Mgonero Wa Ambuye. Adzakumbukukiranso tanthawuzo la mkate ndi vinyo uja, ndi Yesu amene adafa kudzapulumutsa anthu kuchoka ku machimo awo. Yesu adachita kuwafunsa otsatira Ake kuti adzakumbukire imfa Yake pamene anali kunyema mkate ndi kumwa vinyo uja.

## YESU AKONZEKERA KULEPHERA KWA AKUPHUNZIRA AKE

Yesu adawachenjeza Akuphunzira Ake (14:27-30):

- Kuti adzathawa onse;
- Kuti Petro adzamukana katatu
- Kuti Yesu ayenera kufa monga kunalembedwa (Zekariya 13:7).

- Kuti Iye akadzafa ndi kuwuka kwa akufa, adzakumana nawonso ku Galileya kukawafotokozera zonse.

Koma Akuphunzira sanamvetse zinthu izi zonse kufikira zinachitika.

**Kambiranani:**

1. Kodi Akuphunzira adamufunsa mafunso wotani mwini nyumba yomwe Yesu amafuna akadyeremo Mgonero (14:14)?
2. Yesu adamusonyeza bwanji munthu amene ati adzamupereke Iye (14:20)?
3. Kodi Yudasi adachitanji (Mateyu 26:14-16)?
4. Kodi mumakhulupirira zimene Mulungu adanena kuti zidzachitika?
5. Kodi mumamvetsetsa kuchenjeza ndi malonjezano a Yesu?

## Werengani: Marko 14:32-52

## YESU APEMPHERA NDI KUVUTIKA M'MUNDA

Yohane, wophunzira wa Yesu, adatilembera zambiri zimene Yesu ananena pa nthawi imeneyi. Werengani Yohane 14:1 mpaka 17:25.

Yesu adawatsogolera Akuphunzira Ake kuwoloka mtsinje wa Kedron ndi kulowa mu munda wa Getsemane. Mundawu unali pa phiri la Azitona. Kumeneku ndi kumene anali kukonda kupita kukapemphera, akuwona mzinda wa Yerusalemu mu chigwa kotero. Anapita kuti akapemphere kotsiriza ali ndi mtima wachisoni kwambiri.

'Bakhalani pano nimudikire', Iye anawawuza Akuphunzira Ake. Iye anapita patsogolobe kumene anafuna kukakhala payekha ndi Atate Wake. Anali wachisoni kwambiri moti anali kumva ngati akufa.

'Abba, Atate, zinthu zonse zitheka ndi Inu, mundichotsere chikho ichi; komatu sichimene ndifuna Ine koma chimene mufuna Inu' (14:36).



**Jesus ora no Jardim do Getsêmani com grande tristeza enquanto Seus discípulos adormecem**

Yesu anali kumva kuwawa kwambiri mumtima mwake. Machimo a wanthu anali kukamupha! Udani wa atsogoleri azipembedzo unali kumutsogolera ku imfa. Yesu anali kukafa chifukwa cha machimo awo, ndipo sakadatha kulimbana ndi iwowa. Iye anali wolola kupereka moyo Wake monga nsembe yolungama ya Mulungu, kuti mwa Mwazi Wake Mulungu akathe kukhululukira machimo a anthu - nthawi imeneyo, ngakhalenso lero. Izi Yesu adazidziwa. Komabe anali kumva

ululu waukulu mkati mwa moyo Wake, umene posachedwa umayembekezedwa kufalikira pa thupi lake. Yesu adamva zowawa zotere chifukwa cha anthu onse.

Yesu adamva zowawa ndi kufa chifukwanso cha machimo anunso nanu! Chikonzero cha Mulungu chinali chofuna kupulumutsa anthu onse, nthawi zonse, kuli konse. Bwerani kwa Yesu Lero kuti nsembe imene Iye adapereka isapite pachabe. Imfa Yake ndi Mwazi Wake unalipira mtengo wa machimo anu inuyo ngakhalenso machimo a anthu a nthawi imeneyo. Mupempheni Mulungu kuti akhulululukire machimo anu, chifukwa Yesu adafa m'malo mwanu.

Pamene Yesu anali kupemphera, Akuphunzira Ake anagona tulo. Yesu anabwera nawadzutsa ndi kuti: 'Dikirani, pemperani, kuti mungalowe mkuyesedwa; mzimutu uli wakufuna koma thupi liri lolefuka'.

Yesu adachokanso napita kokapemphera. Akuphunzirawo adagonanso. Kachitatu Yesu anabweranso ndi kuti: 'Gonani tsopano, nimupumule; chakwanira; yafika nthawi; onani Mwana wa munthu aperekedwa m'manja a anthu ochimwa' (14:41). Yesu adawona miuni (nyali, nsakali) ndipo anadziwa kuti asilikari anali kubwera kudzamugwira Iye.

Akuphunzira Ake analephera mudikira ndi kupemphera' pa nthawi imene Yesu adawasowa koposa. Iwo sanamvetse chimene chimafuna kuchitika. Ili ndi chenjezo kwa ife kuti: 'mukadikire ndi kupemphera'.

## KUGWIDWA KWA YESU

Nthawi yomweyo, Yudasi anafika ndi alonda a Kukachisi ndi akulu ansembe. Iwo ananyamula malupanga ndi ndodo (14:43). 'Amene ndimupsyopsyone ndi yemweyo; mgwireni', Yudasi anawawuza.

Ndipo Yesu anati kwa iwo' Kodi mwatuluka ndi malupanga ndi mikunkhu kundigwira Ine monga wachifwamba? Masiku onse ndinali nanu Mkachisi ndikuphunzitsa ndipo simunandigwire Ine' (14:49).

Asilikaliwo anamugwira Yesu, koma Iye sanatekeseke. Akuphunzira adafuna kuchita nkhondo. Wina anati: mulimbane nawo ndi malupanga Ambuye?' (Luka 22:49). Koma Yesu sanawalora kuchita nkhondo. Kenaka Akuphunzira anamuthawa. Yesu anamutengera kwa Mkulu wa ansembe kuti akayambe kumuzenga mulandu.

## 📖 Werengani: Marko 14:53-72

## KUYESEDWA KWA PETRO

Nkhani ziwiri zikuperekedwa motsatana: (1) kuweruzidwa kwa Yesu; (2) kuyesedwa kwa Petro ndi m'mene iye anamukanira Yesu. Petro anali kuchita mantha, komabe anatsatira Yesu chapatali (14:54)

Asilikiri aja anamutenga Yesu kupita kubwalo la kunyumba kwa Mkulu wa ansembe. Wina anamulola Petro kulowa nawo. Ali mkatimo mtsikana wantchito anamuzindikira nati: 'Iwenso unali naye Mnazarene Yesu'. Koma Petro anakana nati: 'simukundidziwa kapena kumvetsa chimene uchinena iwe'. Petro anatuluka

nakayima pachipata (14:69; 70). Mtsikanayo anamuwonanso pamene anayimapo nanena ndi ena amene anayimirirapo 'Uyu ndi wa awo'. Petro anakananso.

Kenaka anthu ena analankhula naye nati: 'Indedi uli wa awo; pakutinso uli Mgalileya. Kalankhulidwe kako kakuwulula' (Mateyu 26:73). Petro anayamba kutemberera ndi kulumbira, 'sindikumudziwa ine munthu ameneyu!'. Iye anangomva tambala akulira, ndipo anakumbukira mawu amene ananena Yesu (14:30, 72). Iye anatuluka kunja nalira mosweka mtima. (ayenera kuti anamufotokozera Marko zimenezi pambuyo pake) Sizokwanira kulimba mtima kumutsatira Yesu kokha, koma tisoweka Mzimu Woyera kuti atipatse mphamvu (Aroma 8:26).

**NZERU YA MULUNGU YAKUPULUMUTSA DZIKO**

Mulungu adadziwa kuti Mwana Wake adzaperekedwa:

- Vesi 15: Chipinda chinali chokonzedwa kale chimene adzadyeramo Paskha. (Izi zikusonyeza MALO ndi NTHAWI imene ziti zidzachitike.
- Vesi 18: Munthu wina anali wokonzeka kupereka Yesu. (Umu ndi momwe zidzachitikire)
- Vesi 24: Akuphunzira anawakonzetsera chiyambi chatsopano (mgwirizano) ndi Mulungu kupyolera mu mwazi wa Yesu. (Ichi ndi CHIFUKWA chimene zidzachitikire)

Yesu asanaphedwe anatenga zinthu ziwiri zodziwika nazipatsa tanthawuzo latsopano:

1. **Mkate**, umene umatikumbutsa ife za Thupi Lake. Mkate ndi chakudya chopatsa moyo. Koma kuti utipatse moyowo mkatewo uyenera kunyemedwa. Thupi la Yesu linapwetekedwa ndi misomali, mkondo, kukwapulidwa ndiponso minga koma mafupa ake sanaphwanyidwe.
2. **Vinyo** (madzi wopsyinyidwa ku mpesa), amene amatikumbutsa za mwazi Wake, wokhetsedwa. Mwazi umatikumbutsa za nsembe ndi imfa. Koma imfa ya Yesu imatipatsa ife moyo.

Zinthu ziwiri zimenezi zimapereka chithunzi cha imfa ya Yesu, ndi kutikumbutsa ife zimene Iye adatichitira potifera pa mtanda.(Luka 22:19). Chifukwa cha Thupi Lake lopwetekedwa ndi Mwazi Wake wokhetsedwa, ife tikhoza kukhululukidwa machimo athu. Popanda kukhetsedwa mwazi palibe kukhululukidwa (Aheberi 9:22). Ichi ndi chikonzero cha Mulungu.

## KUWERUZIDWA KWA YESU

Poyamba anamutengera Yesu kwa Anasi mkulu wa ansembe wopuma. Kayafa, mwana wake ndiye amene anali Mkulu wa ansembe wa Bwalo lalikulu la Ayuda. Ndipo anasonkhana kwa iye ansembe akulu onse ndi akulu a anthu ndi alembi (14:53), koma izi sizinachitike mwachilungamo ayi.


Mulandu wa Yesu unazengedwa usiku kumene kunali kulakwira lamulo la Ayuda.

Oweruza a udindo ocheperapo ndiwo anayenera kuyamba kunenapo kanthu, koma apa anangofikira ndi mkulu wa ansembe.

Wozengedwa mulandu sanayenera kutundudzidwa, koma Yesu anamutsira malovu ndi kumumenya.

Ukakhala kuti mulandu ndi wawukulu, woyenera chilango cha imfa, oweruza sanali kuloledwa kupereka chigamulo mpaka tsiku lotsatira.

Bungwe lonse la oweruza kuphatikizapo alembi, ndi aphunzitsi anafunafuna njira yomupatsira mulandu Yesu kuti amupeze wolakwa ndi kumupha Iye (14:55).



**O julgamento de Jesus começa diante do Sumo Sacerdote**

## M'MENE PETRO ANAMUKANIRA YESU

Petro analephera mayeso. Iye anamumvetsa chisoni Yesu pomukana kuti sanali wotsatira Wake. Izi zinachitika pang, onopang'ono koma mwatsatanetsane wotere:

Petro anamutsatira Yesu koma sanafune kuti anthu ena adziwe kuti anali wakuphunzira Wake (14:54).

Petro anali kuwopa kuti angagwidwe ukayidi choncho ananena kuti sakumudziwa Yesu (14:67-71).

Nthawi zonse zimene iye anali nkukana anali kupitirira kupsyerapsyera mtima (14:71).

Petro analira kwambiri pamene anakumbukira zimene Yesu ananena kwa iye (14:72)

Motero Yudasi anamupereka Yesu, Petro anamukana ndi Akuphunzira ena onse anathawa. Tikuwona kuti Akuphunzira onse khumi ndi awiri anamukhumudwitsa Yesu. Yudasi anataya chikhulupiriro chonse kuti angakhululukidwe ndipo adadzipha yekha, koma ena onse anamva chisoni nabwerera kwa Yesu. Yesu anamukhululukira Petro ndi ena onse khumi aja ndipo anawagwiritsa ntchito ya kumanga mpingo Wake pa dziko lapansi. Mu bukhu la Machitidwe, timawerenga za zimenezi ndiponso kuti Petro anadzakhala mtsogoleri wa mpingo ku Yerusalemu.

Ambiri adapereka umboni wonama omupachika Iye, koma sanamupeze ndi mulandu. Yesu analibe tchimo (Ahebri 4:15).

Mboni zonama zambiri zinayitanidwa kudzatsutsana naye Yesu.

Zimene anali kumunenera Yesu sizinali kugwirizana ayi, choncho Mkulu wa ansembe anamufunsa Yesu, muyankha kanthu kodi?' Yesu sanayankhe kanthu pa zamabodzazo. Koma m'mene Mkulu wa ansembe anamufunsa 'kuti kodi ndiwe Mesiya- Khristu, Mwana wake wa Wolemekezeka (Mulungu)?' Iye anayankha kuti 'Ndine amene; ndipo mudzawona Mwana wa munthu ali kukhala ku dzanja lamanja la mphamvu, ndi kudza ndi mitambo ya Kumwamba' (14:61-62).

Mkulu wa ansembe anakwiya. mufuniranjinso mboni zina Bwalo la milandu la Bungwe la Ayuda lidamupeza Yesu wolakwa ndi kumupatsa chirango choti aphedwe. (14:63-64).

Asirikali adamumanga nsalu mophimba maso namumenya ndi mikondo ndi mitengo. Ena anamulavulira malovu. Ananena, lota, 'utiwuze Khristu. Ndi ndani wakumenya?' (Mateyu 26:68).

Apa tikuwona kulimba mtima kwa Yesu. Iye anadziwa chifukwa chimene anadzera pa dziko: 'mwana wa Munthu sanadza kudzatumikiridwa ayi, koma kudzatumikira ndi kudzapereka moyo wake ngati mtengo wowombolera anthu''(10:45).

Mulandu wa Yesu unazengedwa usiku. Uku kunali kulakwira malamulo a Chiyuda. Kenaka anamumanga Yesu namutengera Iye kwa Pilato, wolamulira wa Chiroma wa dera la Yudeya. Ndi Pilato yekha amene anali ndi udindo wolamula munthu kuti akapachikidwe.

**Kambiranani:**

1. Ndi tsiku liti limene Yesu adzabweleranso kachiwiri ndipo dziko lonse lidzamuona (13:26)?
2. Fotokozani mau a Yesu amene anayankha mpaka kufika poti akulu a nsembe ayambe kunena kuti wachitira Mulungu mwano? (14:61, 62)
3. Kumva za Yesu ena amakondwa pamene ena amakhumudwa. Ndinu wokonzeka chichira kuchitira umboni za Yesu?
4. Ndikangati mwakanapo Yesu ngati Petro?
5. Ndi anagati amene zimawavutani kuchitira umboni za Yesu?

## Werengani: Marko 15:1-41

## KUWERUZIDWA KWA YESU NDI MKULU WA CHIROMA

Atsogoleri achipembedzo anamuwuza Pilato zimene adamutsutsa nazo Yesu. Iwo anati:

- Anali kuwawuza anthu mabodza;
- Anali kuwawuza anthu kuti asamapereke misonkho kwa Kaisara;
- Anali kuwawuza anthu kuti Iye ndi mfumu;

- Anali kuwawuza anthu kuti Iye ndi Mesiya, wodzozedwa wa Mulungu (Luka 23:1-2).

Iwo adayankhula mawu a udani, koma Yesu sanawade adani Ake kapenanso kuwayankha.

Pilato analibe chidwi mu chipembedzo cha Ayuda, koma iye anangofuna kudziwa ngati Yesu anali kunenadi kuti Iye ndi Mfumu. 'Kodi iwe ndiwe Mfumu ya Ayuda?' iye anafunsa Yesu. 'Mwatero', anayankha Yesu (15:2). Koma Yesu anamuwonetsera Pilato kuti Iye sanali monga mfumu wamba monga ena amdziko (Yohane 18:36).

Bwalo la akulu a msembe anafunafuna umboni wonama wakumupachika Yesu. iwo sanadziwe za choonadi. Pilato anafunsa Yesu'Kodi iwe ndiwe Mfumu? Yesu anayakha, Munena ndinu kuti ndine mfumu. Ndinabadwira ichi Ine ndipo ndinadzera ichi kudza padziko lapansi kuti ndikachitire umboni wa choonadi. (John 18:37). Chocho chifukwa chonena kuti anthu anakana choonadi mapeto ake anthu anakana mwana wa Mulungu. Ndipo dziko limene siliwuza anthu ake choonadi limaonaongeka.

Pilato anazindikira kuti Yesu sanali wolakwa. Unali mwambo wa Chi Roma kumasula m'modzi wa akayidi pa tsiku la chikondwerero cha Paskha. Pilato sanapeze cholakwa mwa yesu choncho anali kufuna kumumasula. Iye anawafunsa anthuwo kuti amasule yani: Baraba wachifwamba kapena Yesu?

Mkulu wa ansembe anakakamiza gululo (15:11). Phokoso linakula pamene gululo limafuwula kuti awamasulire Baraba ndi kumupachika Yesu. (15:13) Pilato anafunsa kuti Yesu anachita choyipa chotani? (15:14)

## PILATO ASAMBA M'MANJA

Gulu la anthulo linafuwula kwambiri ndipo Pilato anawopa kuti anthuwo ayambitsa zipolowe. Iye anatenga beseni la madzi ndi kusamba manja ake pamaso pa khamu lonse. 'Ine ndiribe tchimo pa imfa ya munthu uyu, (Mateyu 27:24). Anthu onsewo anafuwula kuti mwazi wake udzakhala pa ife ndi ana athu (Mateyu 27:25)

Khamulo linali kulolera kutengerapo thayo pa imfa ya Yesu. Chotero Pilato anamasula Baraba, wakupha koma analamula kuti Yesu akwapulidwe.

Asilikaliwo anachoka naye Yesu nalowa m'bwalo, namuvula zovala zake ndi kumuveka chibakuwa, naluka korona wa minga nayika pa Iye kuti awoneke ngati mfumu. Anamuchitira chipongwe nalavulira malovu pa Iye ndi kumumenya pa mutu ndi mitengo mobwerezabwereza.

## KUPACHIKIDWA KWA YESU

Anamusenzetsa mtanda pa mapewa ake namuwuza kuti awunyamule kufikira Iye anagwa nawo. Kenaka anatenga munthu wodutsa Simoni wa ku Kurene (Kumpoto kwa Afirika). Munthu ameneyu anali atayenda mitunda chikwi kuti akakhale nawo pa Paskha ku Yerusalemu. Iyeyu anakakamizidwa kunyamula mtanda wa Yesu (15:21). Atafika paGolgota, Malo a Bade, pamenepo

anamupachika Yesu pomukhomera pa mtanda wa mtengowo ndikumukhoma ndi misomali (15:22-24).

### *1. Asilikali ndi Yesu*

Asilikali a ChiRoma sanali kulabadira kuti akupha ndani, kaya akuchita nkhanza chotani. Kwa iwowa Yesu anali monga wina aliyense wolakwira lamulo. Anamunyodola ndi kumukwenzulira pakamwa. Atapempha madzi anamupatsa vinyo wosasa (15:36).

'Tiyeni tisang'ambe chovala chake, koma tichite mayere kuti tiwone amene achitenge,' wina ananena (Yohane 19:24). Chovalachi chinalibe msoko kuyambira pamwamba mpaka pansi (Yohane 19:23).

Zolembedwa zopatulika zinalosera: 'Iwo anagawana chovala Changa pochita mayere' (Masalimo 22:18) Iwo anadikira kuti Yesu afe. Pamene anali kumuyang'ana Iye anawapempherera: 'Atate, akhululukireni popeza sadziwa chimene achita' (Luka 23:34).

### *2. Anthu ena Pafupi ndi Mtanda*

Awa anali: Gulu longochita chidwi; wokhulupirikawa, anati kwa amayi Ake Amayi, wonani mwana wanu'. Ndi kwa wakuphunzira Wake Yohane Iye anati, Ona mayi wako awa' (Yohane 19:26-27). Chotero Yohane anamutenga Mariya kupita naye kwawo kukamusamalira. Pa nthawiyi Mariya anali wamasiye.

### *3. Mbala Ziwiri Zopachikidwa pa Mtanda Pafupi ndi Yesu*

Mbala ziwiri zinapachikidwa pa mitanda wina kumanja mzakeyo kumanzere kwa mtanda wa Yesu. Amuna awiriwa analankhula ndi yesu. M'modzi anali woyipa ndi wowawidwa mtima. Iye anamunyodola Yesu ndi kuti: 'kodi sindiwe Khristu Iwe? Dzipulumutse wekha ndi kupulumutsa ifenso' (Luka 23:39). Izi zinakhumudwitsa mzakeyo. Iye anamudzudzula ndi kuti: 'kodi iwe suwopa Mulungu, powona uli nkulangika komweku? Ndipo ifetu kuyenera pakuti tiri kulandira zoyenera zimene tinazichita: koma munthu uyu sanachite kanthu kolakwa'. (Luka 23:40-41). Yesu anamukhululukira machimo ake munthu ameneyu (Luka 23:43).

Ndipo mbala ya chiwiriyi inachewukira kwa Yesu ndi kupempha: mundikumbukire ine pamene mulowa Ufumu Wanu.(Luka 23:42) Kwa iyeyu Yesu anati: 'Chimene ndikuwuza iwe lero, ndi chowona. Udzakhala ndi Ine mu paradizo.' (Luka 23:43).

## ZOZIZWITSA ZA PA MTANDA

Tawonani kuti Yesu analirira kwa Mulungu, Atate Wake. Yesu anali kumva kuti watayika ndi kusiyidwa ndi Mulungu. Iyi inali mbali ya kunzunzika pa mtanda. Pamene Yesu anamwalira, Mulungu anatumiza zizindikiro zazikulu ndi zodabwitsa:

Mdima wa pakati pa usana (Luka 23:44-45). 'kuyambira ola la chisanu ndi chimodzi mpaka ola la chisanu ndi zinayi, mdima udaphimba dziko' (Mateyu 27:45). Dzuwa silinakwere mlengalenga, koma mdima unagwa pa dziko.

### Mulandu wa Yesu

Mulandu wa Yesu unachitika usiku umodzi koma unali ndi zigawo zambiri. Iye anafunsidwa mafunso ndi Ayuda katatu, ndi Aroma katatunso:

Yesu pamaso pa Anasi, Mkulu wa nsembe wopuma (Yohane 18:12-13).

- Kayafa, Mkulu wa ansembe, anamuzenga mulandu kutatsala pang'ono kucha (Yohane 18:24).
- Kuzengedwa mulandu ndi Akuluakulu a Chiyuda (Marko 14:60-64)
- Kuzengedwa pamaso pa Pilato (Luka 23:1-5).
- Kuzengedwa pamaso pa Herode (Luka 23:7-11).
- Kuzengedwa kotsiriza pamaso pa Pilato (Luka 23:13-25)

(Mdima wa ma ola atatuwu unafika mpaka ku Roma, mtunda wotalika mitunda chikwi, monga zinawonetsedwa ndi katswiri wolemba mbiri yakale – Thallus).

Nsalu yotchinga pa kachisi, imene inalekanitsa anthu wamba ndi Mulungu, inang'ambika pakati kuyambira pamwamba mpaka pansi. Anthu tsopano akhoza kubwera kwa Mulungu mwa chindunji, chifukwa cha nsembe ya Yesu (Ahebri 9:12; 10:19-20). Sitisowanso kuti mkulu wa nsembe azipita kuseri kwa chinsalu chotchinga mu Kachisi kapena tchalitchi kukafunsa Mulungu kuti atikhululukire

machimo athu. Yesu ndiye Mkulu wa Nsembe wathu. Kupyolera mu Mwazi Wake ndi Imfa Yake ife tikhoza kufika kwa Mulungu.

Chivomerezi: chozizwitsa china chinali chivomerezi. Nthaka inagwedezeka ndi matanthwe anasweka' (Mateyu 27; 51). Mulungu anagwedeza dziko ndi mphamvu Yake yayikulu.


Manda a muderalo anatseguka ndipo anthu a Mulungu ambiri adakhalanso ndi moyo (Mateyu 27:52). Mizimu yawo ndi matupi awo zidalumikizana ndi kukhalanso ndi moyo! Kunali chimwemwe chachikulu Kumwamba pamene anthu woyerawa anatuluka m'manda mwawo. Yesu atawuka kwa akufa, iwo analowa mu mzinda kukawonetsa kuti Mpulumutsi wawo wawuka! Ali ndi moyo anali anthu a Mulungu, ndipo Mulungu anawagwiritsa iwo ntchito ngakhale kuti analawa imfa.

## M'MENE MTANDA UDASINTHIRA MBIRI YA DZIKO

Chipangano Chakale chimanena m'mene Mulungu ati adzatumizire munthu kudzapulumutsa anthu Ake kuchoka ku machimo awo. Chipangano Chatsopano chimanena m'mene Khristu anafikira ndi kufa ndi kuwuka kwa akufa kuti ife tikakhululukidwe (Aefeso 4:32).

Kwa anthu ambiri lero mau oti mtanda samatathauza kathu pa moyo wawo koma tikuyiwala dala kunena kuti palibe chipulumutso mwa wina yense koma Yesu mwa yekha, Tonse tinayenera kufa chifukwa cha zolakwa zathu popeza kuti tonse tinachimwa (Romans 3:9, 10). Koma Mulungu anatikonda ife ndipo

sanatichire monga mwa zolakwa zathu kapena kutibwezera monga mwa mpulumulu zathu (Psalm 103:10-12). Koma pokhala ife chikhalire ochimwa Khristu adatifera ife (Romans 5:8). Ndipo aliyense amene adzichepetsa yekha navomeleza zochimwa zake ndikukhulupilra kuti Yesu anafa chifukwa cha ife. Moyo wake umayenera kusitha. machimo ake amakhulukidwa ndipo Mulungu samakumbukiranso. Pamene ayandikira kwa Mulungu amakhala wofanafana naye Yesu ndipo amakhala ndi chiyembekezo cha moyo wosatha kumwamba.



**A crucificação do Filho de Deus com dois criminosos**

**Yesaya Enalemba**

Iye anatsenderezedwa koma anadzichepetsa yekha osatsegula Pakamwa pake; ngati nkhosa Yotsogoleredwa kukaphedwa, ndi ngati nkhosa pamaso pa omsenga motero sanatsekula pakamwa pake (Yesaya 53:7)

## Werengani: Marko 15:42-47

## KUKHALA NDI MATUPI WOTETEZEDWA

Itachitika imfa ya Yesu, zinthu zinachitika mofulumira kwambiri chifukwa dzuwa linali litatsala pang’ono kulowa pa tsiku la Lachisanu (Friday) madzulo. Popeza uku kunali kuyamba kwa Sabata la Ayuda amene sanali kulola kuti ntchito iriyonse idzigwiridwa Sabata likayamba.

Mariya ndi Mariya wina anawonerera pamene Yosefe wa ku Arimateyo anali kutsitsa mtembo wa Yesu kuchoka pa mtanda. Pilato anamupatsa Yosefe chilolezo kuti akayike m’manda mtembo wa Yesu.

Yosefe anawukutira mu nsalu yoyera bwino mtembowu nawuyika m’manda. Manda ake anali ngati kachipinda kakang’ono kosemedwa ku mwala kumene amayikako anthu akufa. Yosefe anakankha mwala wawukulu umene anatseka nawo pa khomo la mandawo. Iye anachoka nasiya azimayi awiri aja atangokhala panja pa mandawo.

Tsiku lotsatiralo Pilato analamula asilikali ake kuti akalondere mandawo kuti wina aliyense asakabemo thupi la Yesu.

Nanena, Mfumu takumbukira kuti ife kuti wonyenga uja anati pamene anali ndi moyo; Ndidzauka pofika masiku atatu (Mateyu 27:63). Koma wophunzira sanakumbukire ichi. Ndipo sanadziwe kathu za izi ndi mau awa adawabisikira, ndipo sanazindikira zonenenedwazo (Luke 18:34).



**O sepultamento de Jesus no túmulo de José assistido por um soldado romano e as duas Marias**

## Werengani: Marko 16:1-14

## YESU KHRISTU AWUKA KWA AKUFA

Mwawa wa tsiku la Sabata (Sunday) azimayi atatu anatenga zonunkhiritsa (Masamba owuma a mitengo yonunkhira). Iwo anapita ndi zonunkhiritsazi kumanda kumene anayikako mtembo wa Yesu. Iwowa anafuna kuwaza zonunkhirazi pa mtembowo. Pamene anayandikira kumandako, anayamba kufunsana wina ndi mzake ndi ndani amene ati akatikunkhunizire mwala pa khomo la manda?'(16:3). Mwala umene anatseka nawo khomo la manda unali wawukulu ndi wolemera. Koma atapenyetsetsa anawona kuti mwalawo unali utachotsedwapo kale. Mngelo wa Mulungu anali atakunkhuniza mwalawo (Mateyu 28:2).

Ndipo mngeloyo ananena nawo: Musadabwe; muli kufuna Yesu… Iye sali pano; tawonani mbuto imene anayikamo Iye. Pitani msanga mukawawuze akuphunzira Ake kuti Iye wauka kwa akufa'. Apa tiwona kuti mngelo unatchula makamaka Petro, amene anamukana Yesu (16:7) osati Yudasi amene anamupereka Yesu. Mngeloyo ananena kuti Yesu apita ku Galileya kukakumana ndi



**O anjo de Deus mostra às mulheres o túmulo vazio para provar que Jesus havia ressuscitado da morte**

akuphunzira Ake — monga Iye anakuwuzirani inu' (16:7).

Azimayi aja anachoka kumandako akuthamanga, ali ndi mantha komanso atadzazidwa ndi chimwemwe. Atafika ku mzindako, anawafotokozera Akuphunzira khumi ndi m'modzi kudzanso ena za zimene anawona ndi kumva. Koma iwo sanakhulupirire (Luka 24:11).

## YESU AONEKERA KWA AKUPHUNZIRA AKE

Petro ndi Yohane anathamangira ku manda. Yohane anali woyamba kufikako. Iye anasuzumira nawona nsalu zimene adamukulungira zija, koma sanalowamo. Petro amene anamutsata Yohane pambuyo anafikira kulowa m'mandamo. Iye anawona nsalu zimene anamufunditsa nazo ndi zimene anakulunga nazo mutu wa Yesu. Nsaluyo inali yopindidwa iri potero. Iwo pamene atawona nsaluzo anadziwa kuti Yesu anawuka! (Yohane 20:6-8).

Mariya wa Magadala anabwereranso kumandako nayima kunja ndi kuyamba kulira. Kenaka anawona munthu. Iye anaganiza kuti anali woyang'anira munda. ngati mwawatenga Ambuye, ndiwuzeni kumene mwakawayika Iwo iye anadandawula. Kenaka Yesu anayankhula nati 'Mariya'. Mariya anawazindikira mawuwo! Iye anagwada pansi namulambira Iye, atagwira mapazi Ake.

Yesu anati, 'Usandikhudze; pakuti sindinatha kukwera kwa Atate' (Yohane 20:19) Mariya wa Magadala anafulumira kupita kwa akuphunzira ena.

Madzulo womwewo, Akuphunzira anali muchipinda cha pamwamba. Makomo anali wotseka chifukwa anali kuwopa atsogoleri a Chiyuda (Yohane 20:20). Atsogoleri achipembedzowa atawona kuti zinthu zasokonekera anawapatsa ndalama asirikali a Chiroma amene anali kulondera manda aja kuti aziwuza anthu kuti akuphunzira ake anamuba (Mateyu 28:12-14)

## ZIMENE YESU ANANENA ASANAKWERE KUPITA KUMWAMBA

Yesu atawuka, akuphunzira ake khumi ndi m'modzi anapita ku Galileya monga m'mene Yesu ndi mngelo uja adawawuzira iwo. Izi ndi ziphunzitso zotsiriza za Yesu:

1. Iye anawawuza kuti, 'Ulamuliro wonse Kumwamba ndi dziko lapansi zapatsidwa kwa Ine' (Mateyu 28:18).
2. Otsatira Ake apite ku mayiko a dziko lonse lapansi ndi kusandutsa anthu kukhala akuphunzira a Yesu.
3. Omutsatira akabatize amene akhulupirira mu dzina la Atate, ndi la Mwana ndi la Mzimu Woyera (Mateyu 28:19).
4. Wotsatira a Yesu ayenera kuphunzitsa zinthu zimene Yesu anaphunzitsa(Mateyu 28:20)
5. Yesu adzakhala nawo anthu ake kwa nthawi zonse (Mateyu 28:20).
6. Iwo amene akhulupirira mwa Yesu adzapulumutsidwa, koma iwo amene sakhulupirira mwa Iye adzalangidwa (Marko 16:16).

7. Iwo amene akhulupira mwa Yesu adzachita zodabwitsa zazikulu ndipo adzapatsidwa mphatso ya kuyankhula malilime (zinenero) achilendo (Marko 16:17).
8. Zonse zonena za Yesu zolembedwa mu mabukhu a Mose, aneneri ndi mu Masalimo zidzachitika (Luka 24:44).
9. Womutsatirawo adzawuza anthu za Yesu ndi kuwaphunzitsa iwo kutembenuka kusiya machimo awo kuti akakhululukidwe (Luka 24:47).
10. Anthu wochokera ku mitundu yonse adzamva za dzina la Yesu (Luka 24:47).
11. Anayenera kuyambira ntchito imeneyi mu Yerusalemu (Luka 24:47).
12. Akuphunzira adzadikire kufikira Mulungu atawatumizira iwo mphamvu Yake yochokera ku Mwamba (Luka 24:49).

## MUTSATENI YESU LERO

Tiyenera kuyesetsa kutsatira malangizo a Yesu. Paulo anayesa kutsatira utumiki wa Yesu. Nachi pano chitsanzo chimodzi chopezeka mu Machitidwe 14:21-23.

- Paulo analalikira uthenga wabwino wa chipulumutso cha Mulungu, kutembenuza ndi kumupezera Yesu otsatira atsopano (v. 21).
- Paulo anaphunzitsa wokhulupirira m'mene angakhalire wolimbikira pa chikhulupiriro chawo ndi kukhala wolimba ngakhale mu nthawi yamavuto (v. 22).
- Paulo anasankha atsogoleri mu mipingo amene anali ndi chikhulupiriro chozama mwa Mulungu (v. 23).
- Paulo anapemphera kwa Mulungu kuti ayang'anire mpingo ndi atsogoleri ake (v. 23).

Pitirizani kuwerenga Baibulo lanu kuti mukamvetsetse zambiri zoyenera kuchita kuti munthu akhale wotsatira wa Khristu ndi momwe tingatumikire mu mpingo wake mwa mphamvu ya Mzimu Woyera.

**Kambiranani:**

1. Kodi mngelo wauthenga ananena chiyani kwa mayi pa manda paja (Mateyu 28:5-7)?
2. Kodi akuphunzira anakhulupirira kuti Mariya anamuwona Yesu?
3. Kodi Mariya wa Magadala anawona woyang'anira munda kapena Yesu (Yohane 20:15)?
4. Uthenga wotsiriza wa Yesu kwa akuphunzira Ake unali woti chiyani (Mateyu 28:18-20)?
5. Mtanda uli ndi tanthawuzo lanji kwa inu?
6. Kodi inu mumamvera mawuthenga otsiriza a Yesu?
7. Kodi anthu mungawawuze bwanji kuti machimo awo akhoza kukhululukidwa?

# YESU AKWERA KUPITA KUMWAMBA

Zitatha zinthu izi akuphunzira adadzazidwa ndi chimwemwe chachikulu (Luka 24:52, 53). Mavesi khumi otsiriza a mu Marko akunena za m'mene Yesu anatengedwera kupita kumwamba (Onani Machitidwe 1:9). Mavesiwa n'utheka kuti analembedwa pambuyo pake popeza sanali mu zolemba zake zoyambirira. Uthenga wa Marko mwina unathera pa 16:8.

Mbiri ya Yesu yochokera kwa Marko ikutha mwadzidzidzi, koma si ikuthera pa imfa ya Yesu ayi. Mbiriyi ikuthera pa zolembedwa za kuwuka kwa akufa ndi malangizo woti apite kokakumana ndi Yesu ndi kupatsidwa malangizo Ake (16:7).

Yesu sanabwererenso kukakangana ndi atsogoleri azipembedzo ndi Pontiyo Pilato. Iye anapita ku Galileya kukaphunzitsa iwo amene anakhulupirira mwa Iye. Iye anawawuza otsatira ake kuti: pitani ku dziko lonse la pansi ndi kukalalikira Uthenga Wabwinowu kwa aliyense' (16:15). Iyi ndi mbali ya kutuma kwa Mulungu kwa otsatira Ake'.

Yesu tsopano anali wokonzeka kuyambitsa mpingo wake. Mbiri ya Mpingo wa Yesu ndi nthano ya anthu onse amene amakhulupirira Iye amene ali ndi Mzimu Woyera.

Mbiri ya zaka zowerengeka zoyambirira za Mpingo wa Khristu inalembedwa kuti ife tidzayidziwe ndi Luka mu bukhu lake 'la machitidwe a Atumwi'.

Mpingo wa Yesu Khristu udzakhalabe chifukwa cha chikhulupiriro mwa Ambuye Yesu wowukitsidwa.

Panagwa m'dima pa dziko lonse lapansi kwa ma ora atatu

### UMBONI WOTSIMIKIZIRA KUTI YESU ANAWUKA

Yesu atawuka, anawonekera kwa anthu nthawi khumi ndi ziwiri:

1. Mariya anakumana ndi Yesu (Marko 16:9; Yohane 20:14-17).
2. Mariya ndi Mariya wina anamuwona Yesu (Mateyu 28:1, 8-10).
3. Yesu alankhula ndi Petro (Luka 24:34).
4. Yesu awonekera pa njira ya ku Emmau (Marko 16:12; Luka 24:13-32).
5. Yesu awonekera kwa akuphunzira ake (Luka 24:36-49)
6. Yesu awonekera makamaka kwa Tomasi (Yohane 20:26-29)
7. Yesu awonekera kwa Akuphunzira Ake asanu ndi awiri pa nyanja ya Galileya (Yohane 21).
8. Yesu aphunzitsa Akuphunzira Ake khumi ndi m'modzi pa phiri (Mateyu 28:16).
9. Yesu akumana ndi wotsatira Ake pa chakudya (Machitidwe 1:4).
10. Yesu awonekera kwa wotsatira mazana asanu (1 Akorinto 15:6).
11. Yesu awonekera kwa Yakobo, mbale wake (1 Akorinto 15:7).
12. Yesu awonekera kotsiriza pamene anali kukwera kumwamba (Luka 24:50-51).




**Jesus volta ao Céu para sentar-se à direita de Seu Pai Celestial para mediar por Seus seguidores na Terra**

[Mark part 2 1e Chichewa rev 2020, revised 2024]

**Publicado por:**
Manna Publications (UK)

**Composição tipográfica:**
MissionAssist (UK)

**Distribuído por:**

**Imprimido por:**

**Deus permitiu que os comentários do ensino da Bíblia de Manna fossem publicados em:**

África do Sul, Angola, Armênia, Benin, Bulgária, Burkina Faso, Burundi, Camarões, Camboja, Chade, R. D. Congo (Kinshasa e Katanga), Congo Rep. (Brazzaville), Costa do Marfim, Egito, Etiópia, Gana, Guatemala, Guinea Ecuatorial, Haiti, Índia, Quénia, Kosovo, Libéria, Malawi, Mali, México, Mongólia, Moçambique, Myanmar, Nepal, Níger, Nigéria, Paquistão, Ruanda, Sérvia, Serra Leoa, Sudáfrica, Sudão, Suazilândia, Tanzânia, Togo, Uganda, Zâmbia e Zimbabwe

**e mais 43 idiomas incluindo 2 em Braille.**

www.manna-publications.org.uk
**Baixe mais de 20+ comentários Maná de ensino da Bíblia gratuitamente**

Também em Francês, Português e Espanhol

Organização principal '**Manna Publications' (EUA):**
www.mannapublications.org

Afiliado a **Avail,** UK organización benéfica registrada no Reino Unido 1017386

## MARKO GAWO 2, Mutu 9 mpaka 16
## Kufa, Kuuka Ndi Kukwera Kumwamba Kwa Yesu Khristu

| | |
|---|---|
| • **Kuwala kochokera kumwamba kunawala pa Yesu**<br>• **Mizimu yoipa ndi machilitso**<br>• **Yesu aneneratu za kutsogolo** | • **Amugwira Yesu**<br>• **Tathauzo la mtanda**<br>• **Tichite chiyani kuti tinkondweretse Yesu tsiku ndi tsiku.** |

**BUKU** ili tikuphunziramo zambiri za mazunzo a Yesu Khristu; kupachikidwa, kuuka ndi ndi kukwera kupita kumwamba- likufotokoza bwino mwa tsatanetsatane m'mene Yesu anafera, kudzuka komanso m'mene ananyamukira kubwerera kwa Atate kumwamba. Mulungu anachita ichi ngati njira yopulumutsa anthu kumachimo awo. Buku ili likuthandizani kudziwa kuti muli opulumutsidwa pamene mulapa machimo anu ndikuti tsiku lina mudzakwera kupita kumwamba kumene kuli Yesu ndikukhala kwamuyaya. Mvetserani bwino mau onse amene Yesu akulankhula nanu mulitenge ngati chenjezo lanu lomaliza.

**BUNGWE** lotsindikiza mabuku la MANNA limapereka timabuku ting'onoting'ono ta mawu am'baibulo tolembedwa ndi a Fred Morris. Kwa zaka zambiri Fred, ndi mkazi wake Lorna, akhala akuyenda dziko lonse kuphunzitsa komanso kulalikira za uthenga wabwino. Atabwelera kwao analemba uthengawu ndikuwusindikiza nkumagulitsa kumene uthenga wokweza chikhristu ukufunika.

**UTHENGA** wolembedwanso uwu uli mu chichewa chomveka bwino chomwe chithandiza kumvetsa komanso kutanthauzira mu zilankhulo zina. Uthandizanso owerenga onse kumvetsa chiphunzitso cha chikhristu ngakhalenso ana a sukulu ya ubusa, aphunzitsi komanso alaliki.

**MABUKU** awa atha kugwiritsidwa ntchito pa inu nokha komanso pagulu. Akuphunzitsani kudziwa choonadi cha Mulungu. Akuthandizani kum'dziwa Yesu Khristu ngati Mwana wa Mulungu. Akuthandizaninso kukamba za chikhulupiliro chanu ndi Mulungu wanu. Akuthandizani kusaleka njira yanu nthawi zonse. Akudziwitsani za chinthu chabwino kapena choipa. Akudziwitsani za zomwe Ambuye amakonda ndi zomwe sakonda.

**NDI PEMPHERO** lathu kuti mukhale ndi mtendere komanso ndi cholinga ndi moyo wanu pamene muwerenga Bukhu Lopatulika pogwiritsa ntchito timabukuti.


# Manna Publications

**MAZIKO A NDEMANGA ZA BAIBULO**

**"Chinsinsi cha Ufumu wa Mulungu pakati pathu." (Marko 4:11)**